

File Copy

1988
By M. G. FRAY and J. R. CHEYNE



INU-NDI KUKOKA M'YOYO
YOTAICA KWA KRISTU



Baptist Publishing House

OF THE BAPTIST MISSION OF ZAMBIA
P.O. BOX 1995 LUSAKA

File Copy

1988
By M. G. FRAY and J. R. CHEYNE



INU-NDI KUKOKA M'YOYO

YOTAICA KWA KRISTU



Baptist Publishing House

OF THE BAPTIST MISSION OF ZAMBIA
P.O. BOX 1000 LUSAKA

INU-NDI KUKOKA MIYOYO
YOTAICA KWA KRISTU

alembi

Marion G. Fray

ndi

John R Cheyne

izo, ali wamkulu ndi onse, ndipo palibe wina angathe kuzikwatula m'dzanja la Atate."

Aefeso 2:4-5: "Koma Mulungu, wolemera cifundo, cifundo ca cikondi cace cacikuru cimene anatikonda naco, tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Kristu (muli opulumutsidwa ndi cisomo."

Akolose 3:5: "Cifukwa cace fetsani ziwalozi ziri padziko, dama, cidetso, cifunitso ca manyazi, cilakolako coipa, ndi cisiriro, cimene ciri kupembedza mafano,"

Aroma 8:1-2: "Cifukwa cace tsopano iwo akukhala mwa Kristu Yesu alibe kutsutsidwa. Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimasula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa."

(5) "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko" (Macitidwe 1:8).

(6) "Potero, ngati inu, okhala oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, koposa kotani nanga Atate wanu wa kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akupempha Iye?"

(7) "Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano" (Mateyu 28:19-20)

MAFUNSO OBWEREZA NDI MAU A MULUNGU OPHUNZIRA

Mutu wa Khumi ndi Ciwiri

1. Chulani zina zomwe ziri cimwemwe cakukhala wocitira umboni.
2. Chulani njira zocepa zina zomwe phunziro iri lakuthandizani, ndi kunena momwe mudzalizgwiritsira nchito zomwe mwaphunzirazi.

Mau a Mulungu Ophunzira (Poyamba yambani mwalemba nzere pansi pa mavesi mu Buku Lopatulika lanu.)

1 Akorinto 15:3-4: "Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristu anafera zoipa zathu monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa tsiku lacitatu, monga mwa malembo."

Yohane 10:27-29: "Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine. Ndipo Ine ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzaonongeka ku nthawi yonse, ndipo palibe munthu adzazikwatula m'dzanja langa. Atate wanga, amene anandipatsa

ZA MKATIMU

MUTU	1.	UDINDO WA KUKOKA MIYOYO YA ENA	1
MUTU	2.	MAKONZEKELO AKUKOKA MIYOYO.....	7
MUTU	3.	KUFUNIKA KWACE KWA MAU NDI MOYO WODZIPEREKA.....	14
MUTU	4.	M'MENE MUNGAGWIRITSIRE NCHITO BUKU LANU LOPATULIKA.....	19
MUTU	5.	ZOKUTHANDIZANI INU NDI ZITSANSO ZOMWE MUNGACITE.....	23
MUTU	6.	MAFIKIDWE ANU.....	33
MUTU	7.	KUPEREKA NJIRA YA CIPULUMUTSO.....	38
MUTU	8.	MASAMALIDWE A UDINDO WA KUZIPEREKA.....	43
MUTU	9.	M'MENE MUNGACITIRE NDI ZIPHUNZITSO ZONYENGA ZA CIPULUMUTSO.....	47
MUTU	10.	MACITIDWE A PA ZA KUPEREKA ZIFUNIKA.....	53
MUTU	11.	UDINDO WACE KWA MUNTHU WATSOPANO.....	61
MUTU	12.	MPHOTHO YA MWA ANTHU OTEMBENUKA TSOPANO.....	67

MAU OYAMBA

KUKOKA MIYOYO YA ANTHU ENA sikakonzedwe ka munthu kuti akhale ndi cikoka ca anthu ena ku dongosolo la zolinga zace. Ndi dongosolo la Mulungu lopulumutsa mizimu yokufa. Ndi dongosolo la Mulungu lopezera ndi kupangira ana auzimu. Ndi yofunikira ana a Mulungu kugawira ena cikondwerero cawo mwa Kristu. Mwina ife tikhoza kukhala ciwalo cofoka, kapena tikhoza kukhala olimba, komabe ife ndife mbali ya dongosolo la Mulungu. Ngati tiri Akristu acilungamo tidzakhala wocitira umboni.

Colinga ca kabuku aka ndi cofuna kukuthandizani inu monga Mkristu kuti muone malo anu m'dongosolo la Mulungu, ndi kuti mukhoze KUKWANIRITSA malo anu omwe angakondweretse Ambuye. Buku iri siliri ndi colinga cobweretsa njira ya "kagulitsidwe" ka zinthu kwa anthu pa cinthu cina. Ndi longothandiza kuika dongosolo lomwe tiri kutsimikiza kuti ndidongosolo labwino locitira umboni za Buku Lopatulika lomwe liri ndi mbiri yabwino m'dziko - dongosolo la Mulungu la ciombolo.

Ife tinatenga cithandizo kucokera m'njira zosiyanasiyana kuti buku limeneli lipangidwe, ndipo tiyamika ndi kuthokoza.

B.F. and J.C.

(Afilipi 2:5-9). Monga Yesu adadzikhuthura yekha pa imfa ya pamtanda cifukwa ca otaika, ifenso tiyenera kukhala ndi malingaliro omwewo. Ngati Ambuye Yesu adafera ocimwa, ndikhulupirira ife tikhoza kukhala m'moyo wacitsanzo cabwino. Afilipi 3:10: "Kuti ndimzindikire Iye, ndi mphamvu ya kuuka kwace, ndi ciyanjano ca zowawa zace, pofanizidwa ndi imfa yace." Tikatero ndiye kuti tiri amodzi ndi Iye.

(3) Cimwemwe cakukhala ndi mphamvu yofanana. Macitidwe 1:8: "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko." Yesu adatumiza Mzimu wace Woyera kwa Akristu apa dziko lapansi kweni kweni pa colinga cimodzi mphamvu yocitira umboni. Ndiye kuti Kristu amapatsa mphamvu okhulupirira ndi Mzimu wace, ndipo iye amakhala mbali imodzi wopatsa mphamvu zida zotengerazi. Taonani cimwemwe cace!

2. CIMWEMWE CA KULEMERA KWA MALONJEZANO.

(1) "Wodala munthuyo wosayenda mu uphungu wa oipa, kapena wosaimirira m'njira ya ocimwa kapena wosakhala pansa pa bwalo la onyoza. Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace; ndipo m'cilamulo cace amalingirira usana ndi usiku. Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; wakupatsa cipatso cace pa nyengo yace. Tsamba lace lomwe losafota; ndipo zonse azicita apindula nazo" (Salmo 1:1-3).

(2) Ndipo aphunzitsi adzawala ngati kunyezimira kwa thambo; ndi iwo otembenuza ambiri atsate cilungamo ngati nyenyezi ku nthawi za nthawi" (Daniel 12:3).

(3) "Iye amene ayendayenda nalira, ponyamula mbeu yakufesa; Adzabweranso ndithu ndi kupfuula mokondwera, alikunyamula mitolo yace" (Salmo 126:6).

(4) "Koma wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye" (Yakobo 1:5).

zinthu zirinkudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale colengedwa cina ciri conse, sicingadzakhoze kutisiyanitsa ife ndi cikondi ca Mulungu, cimene ciri mwa Kristu Yesu Ambuye wathu.

Yohane 3:19: "Koma ciweruzo ndi ici, kuti kuuni-ka kunadza ku dziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima koposa kuunika; pakuti nchito zao zinali zoipa."

Cibvumbulutso 20:15: "Ndipo ngati munthu sana-pezedwa wolembedwa m'buku la moyo, anaponyedwa m'nyanja ya moto."

Mutu wa Khumi ndi Ciwiri

MPHOTHOTHO YA MWA ANTHU OTEMBENUKA TSOPANO

Inu mwabereka mbeu ya mtengo wa patali, kudera nkhwana ndi kulira, ndipo mwapindurapo mbeu yatsopano. Cimeneci ndicotsogozedwa mwa cifuniro ca Mulungu. Iye Akristu tinabadwanso kuti tikhale malo ace okhalamo. Pamene Iye akhala mwa ife, ife timasanduka kukhala mboni. Cimeneci cimayenera kuoneka. Ngati Ambuye akhaladi mwa ife ndikuti akutidzaza ife, tiri mboni zace. Iye amadzicitira umboni yekha mwa ife. Ndimwayi waukulu kwambiri kuti ife tikhale mboni zace, Tiyeni tione ubwino ndi mwayi wina wa cimwemwe ndi mphotho za kukhala mboni zace. Mwina zimenezi zikhoza kutilimbikitsa kuti tikhale wocitira umboni ndi khama.

1. CIMWEMWE CAKUTSIMIKIZA KUKHALA NDI KRISTU,

(1) Cimwemwe cokhalira pamodzi ndi kugawana nchito. Yesu adauza ophunzira ace kuti mu njira yomwe Atate adamutumizira Iye, Iyenso adawatumiza iwo (Yohane 20:21). Ndiye kuti timakhala ndi mwayi wogawana ndi Yesu pocitira umboni kwa otaika.

(2) Cimwemwe cokhala ndi mtima ndi maganizo amodzi

MBALI 1

POKOKA MIYOYO YA ENA NDI INU

MUTU 1

UDINDO WA KUKOKA MIYOYO YA ENA

Mulungu adayenera kukhala ndi munthu wofalitsa Uthenga. Iye akanakhoza Mbiri ya Bwino ya Cipulumutso, koma Iye sanatero. Iye anasankha kugwiritsa nchito anthu ace. Cifukwa cace onani:

1. - Udindo wanu wokoka miyoyo ya ena.

Kodi inu munazindikira cimwemwe cakucitira umboni kwa wina za Ambuye ndi mphamvu yakupulumutsa yace? Cimeneci ndi cimwemwe ceni ceni - cokondweretsa. Cidasu-ngidwira ana a Mulungu amene amamumvera Iye ndipo amakhala mboni zace. Cimakhala cinthu cokondweretsa ndi mwai wopambana poona munthu wina ali kumasulidwa kucokera mu mdima ndi ukapolo wa cimo. Kodi munaona wina wace ali kucoka mu imfa ndi kulowa m'moyo?



Cimenecitu simwai wanu ndi cikondwerero cokha, komatu ndi udindo wanu. Inuyo ndinu mtumiki wace, yemwe muyenera kucitira umboni kwa aliyense amene Iye amamubweretsa pamaso

panu tsiku ndi tsiku naona makhalidwe anu. Siudindo omwe mungausankhule kapena kuukana, kapena kuti Ambuye anayembekeza kukhala wotero. Iye anangonena kuti, "Mudzakhala mboni zanga..." Nanga ndi cifukwa ciani Ambuye sangayembekezere amene wamasulidwa ku ucimo, wapatsidwa moyo wosatha, ndikumudalitsa ndi cuma ca kumwamba kuti asafune kugawira ena zimenezi? Cikondi ca pa Ambuye Yesu ciyenera kukukakamizani kunena kuti, "Inde, Ambuye, Ine ndidzakutsatani Inu. Ine ndidzakhalala mboni yanu." Ndipo mudzayamba kukwaniritsa colinga ca cipulumutso canu - kukhala monga ocitira umboni za Iye (2 Akorinto 5:14-15).

2. - Lamulo lanu la kukoka miyoyo

Kulamulidwa kwanu kweni kweni si kwa inu kuti mucite umboni. Kulamulidwa kwanu ndikutsata Ambuye Yesu ndi kukhala mboni. Iye analonjeza, ngati mutamutsata Iye, kukupangani kukhala asodzi a anthu (Mateyu 4:19). Kapena, kunena kuti, "...mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: Ndipo mudzakhalala mboni zanga..." (Macitidwe 1:8). Mtumiki amene Ambuye amagwiritsa nchito kupanga ophunzira ace kukhala okoka miyoyo ndi Mzimu Woyera.

Kucitira umboni ndi m'mene uyenera "kukhalira." Sikanthu kena komwe ungakacite. Uyenera kukhala kapena kupangidwa kukhala wocitira umboni, Cifukwa ca ici, ngati usankha kutsata Ambuye Yesu modzipereka kwanthuthu kwa Iye, mukatero Iye amakudzazani ndi Mzimu wace, kuteroko ali kukupangani kuti mukhale mboni yace. Ngati mwadziwa kale Ambuye Yesu muli kulamulidwa kumutsata Iye ndi kumauza ena zomwe mwaona ndi kuzidziwa.

Buku Lopatulika limanena mau ochenjeza kuti ngati ife siticenjeza woipa ndipo woipayo afa mu ucimo wace, mwazi wace udzakhala pamitu yathu (Ezekieli 3:18). Inde, muli ndi udindo ofunika ndi wosasinthika.

(3) Mkristu watsopano amayenera kulimbikitsidwa kuti adziyenda ndi Mkristu wakale pomacezera. Iye amayenera kupatsidwa mpata wakuti akamveko za m'mene iye analandilira cipulumutso kwa ocezeredwawo.

(4) Tsopano umeneu umakhala mwai wanu wothandiza Mkristu watsopanoyo kuti akule m'Cikristu ndi moyo wakuya m'cipembedzo, kuti adzitsogozedwa motheratu ndi Mzimu Woyera ndi kuti aphunzire kufa yekha tsiku ndi tsiku (Aroma 6:11; 1 Akorinto 15:31).

MAFUNSO OBWEREZA NDI MAU A MULUNGU OPHUNZIRA

Mutu wa Khumi ndi Cimodzi

1. Perekani ndime za malembo zina zomwe ziri zifukwa zolimbikitsira munthu wolapa tsopano kuti agwirizane ndi mpingo kapena kuti abatizidwe.
2. Chulani zinthu zinai zomwe ziyenera kucitidwa pa nthawi imene munthu wapanga cisankho cace.
3. Perekani umboni wa munthu wina amene mwalankhula naye za Kristu panthawi ya maphunziro amenewa. Kodi zotsatira zace zinali zotani?
4. Kodi udindo wanu ndi wotani pamene munthu wasankha kale?

Mau a Mulungu ophunzira (Poyamba yambani mwalembe m'nzere panso pa mavesiwa m'Buku Lopatulika.)

Yohane 20:31: "Koma zalembedwa izi kuti mukhulupirira kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupirira mukhale nao moyo mdzina lace."

1 Yohane 5:13: "Izi ndakulemberani kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu."

Aroma 8:38-39: "Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa ngakhale moyo, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu ziripo, ngakhale

2. KUCEZERA KWINA (Kutangotha maola 48);

(1) Muwapatsa mapepa olemba za mau a Mulungu (Mathiraki, mabuku onena za cipulumutso, udindo wa kaperekedwe, ziphunzitso za mpingo, moyo wa tsiku ndi tsiku, yonena za kukhala ciwalo ca mpingo, kukula m'Cikristu.)

(2) Ayambitseni kuti adziphunzira Buku Lopatulika. (Ngati pali maphunziro abwino a Buku Lopatulika kupyolera mu mpingo wanu, mukhoza kuwauza za cimeneci; Mwina mwake iwo akhoza kulangizidwa kuti aphunzire malembo ena pantima.) Ndi cinthu cofunika kuti adziwerenga Mabuku Opatulika awo eni tsiku ndi tsiku ndi mokhazikika. Mwina mukhoza kuwauza kuti adziwerenga buku limodzi mu Masalmo ndi mu buku la Uthenga Wabwino wa Yohane tsiku ndi tsiku.

(3) Athandizeni kuti posacedwa agwirizane ndi ciwalo ca mpingo wanu kapena mpingo wina womwe umakhulupira Cipangano Catsopano umene ali nao pafupi.

(4) Tengani nthawi ya mapemphero ndipo alimbikitseni kuti akhale ndi nthawi yao yapadera ndi kumacita mapemphero apabanja.

3. MAKULIDWE A MTSOGOLO;

(1) Nthawi zonse munthu woyamba cipembedzo tsopano amayenera kumathandizidwa ndi Mkristu wokhwima, mudziwacezera sabata ndi sabata ndi kumapemphera nao ndi kuphunzira Mau a Mulungu ku nthawi yokwana masabata asanu ndi imodzi. Cimakhiza kukhala bwino kumene munthu watsopano mu mpingo ayamba kutumikira ndi kukhala ndi misonkhano ya mapemphero.

(2) Iwo amayenera kulimbikitsidwa kuti adzicezera kalasi ya anthu atsopanokawiri kawiri. Ngati simunawayambitse kuphunzira kalasi ina ili yonse kapena kuwauza mabuku ena abwino a Cikristu, citani zimenezi panthawi ino. Mabuku otere amayenera kukhala alipo pa mpingo wanu, kapena kogulitsira mabuku.

3. - Citsanzo canu ca kukoka miyoyo.

Ambuye Yesu ndiye citsanzo canu pamene muli kufuna kumacita umboni. Iye nthawi zonse anali kudziwa muntima zosowa za mizimu ya anthu. Kwa iye mtundu wa munthu kapena udindo wa nthito ya munthu zinalibe kanthu. Iye anapindula miyoyo ya asodzi, osonkhetsa misonkho wa lamulo mbala, ndipo ngakhale acigololo. Iye anagwiritsa nthito njira yakapinduli-dwe yomwe adawakhozera. Iye anaphunzitsa magulu. Iye anapita nyumba ndi nyumba, Iye anagwiritsa nthito nthano ndi zitsanzo. Iye anacitira umboni pa nthawi ya zakudya. Conco Yesu ndiye citsanzo canu comwe muyenera kutsatira kuti mukhale mboni kwa anthu onse ponse ponse mwa njira iri yonse yomwe mungakhazere (Luka 19:10).

Yesu sadangomacita yekha umboniwu.wa anthu, koma Iye anaphunzitsa ophunzira ace m'njira imeneyi ndi kuwatumiza kwina kwace awiri awiri (Luka 10:1).

4. - Mphamvu yanu pakukoka miyoyo.

Yesu anakulonjezani kuti adzakhala nanu kupyole-ra mu Mzimu Woyera motero kuti akupangeni inu kukhala wokoka miyoyo wopambana. "... Ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano (Mateyu 28:20). Indedi ndi mphamvu yodabwitsa kwambiri ndi yokondweretsa yokudza-zani nayo mu nthito yodabwitsa! "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: Ndipo mudzakhala mboni zanga..." (Macitidwe 1:8). Mphamvu ya Mzimu Woyera yocitira mboni za Yesu (Yohane 15:26), kutsu-tsa ndi cimo (Yohane 16:8), ndi kupereka cidziwitso ca uzimu (I Akorinto 2:10). Mukakhala ogwiritsidwa bwino nthito (comwe ciri kutanthauza ndi cakuti, macimo onse akhululukidwa ndi kudziperekeratu kwa Yesu.) Ambuye adzakudzazani ndi mphamvu yace, Mzimu wace. Ambuye akacita zimenezi ndiye kuti mwapatsidwa mphamvu yocitira umboni. Zikatero Ambuye

amakugwiritsani nchito monga cida cace kapena kunena kuti amadzicitira umboni yekha kupyolera mwa inu.

Muyenera kuphunzira kudalira Mzimu Woyera ndi kukhala mwa Kristu. (Mukatha kuphunzira mutu uno, yambani mwasiya ndipo werengani Yohane 15, ndipo pemphani Mzimu Woyera kuti akuthandizeni kumvetsetsa ciphunzitso ca kukhala mwa Iye.) Inu munasankhidwa ndi Mulungu kukhala womulankhulira. Koma ndi Mulungu mwini amene ayenera kugwira nchito yodabwitsa ya cipulumutso. Cimeneci cikupangani inu kukhala oyenera kudzazidwa ndi Mzimu, amene ali mthenga wace wocitira umboni. Buku Lopatulika limalamulira cinthu comweci: "Ndipo musaledzere, naye vinyo m'mene muli citayiko. Komatu mudzale naye Mzimu" (Aefeso 5:18). Ndiye kuti timakhala anchito anzace a Mzimu Woyera, kapena kukhala zida zimene Mzimu Woyera amazigwiritsa nchito. "Koma pamene wafika Nkhoswe, adzandicitira Ine umboni..." (Yohane 15:26-27). Mzimu pamodzi ndi inu nonse ndinu Ambuye Yesu.

Funso ndi lakuti - Kodi inu mukhoza kudzadzidwa ndi Mzimu motani? Mukhoza kuthandizidwa potsatira makwerero otsatirawa;

1. Kulapadi moona macimo onse, polondora lonjeza-lomwe liri mu 1 Yohane 1:9. Kodi ndi cifukwa ciani muyenera kubvomereza macimo anu onse kwa Ambuye? Yesaya amanena kuti, "... Zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo macimo anu abisa nkhope yace, kwa inu, kuti Iye sakumva" (Yesaya 59:2). Ngati m'moyo mwanu muli cimo, Mulungu sangakugwiritseni nchito. "Ndikadasekera zopanda pace m'mtima mwanga, Ambuye sakadamvera" (Masalmo 66:18). Kodi kubvomereza macimo anu kumatanthauza ciani? Cimatanthauza kuti mumaululira kwa Ambuye ndi kuona macimo monga momwe Iye amawaonera. Simuyenera kubisa cimo liri lonse, koma kuulura cimo liri lonse ndi kuliika pamaso pa Ambuye ndi kuika pamaso pa Ambuye limodzi ndi limodzi pa Yesu, amene anawafera. Ngati cimo lanu lidakhudzapo munthu wina, kupepesa kapena ciya-

KADI YA KUFUNA FUNA WOTAICA

DZINA LAKHOLO Banda DZINA LA CIKRISTU Joel

Keyala Mateo (Nambala ya nyumba) 2/4

Malapidwe anu ndi otani:-

Kukhulupirira Kristu ✓

Kudziperekanso ✓

Kapena pali zina ✓

Cilankhulo Cewa

Mpingo umene Baptist

Mwalapiramo Ya akulu

Dzina la Sukulu Ya akulu

Tsiku 22 May 1972



- (4) Mudzisonkhanitsa nkhani. (Mudzilemba pa pepala la kakadi ngati kungatheke.)
- (5) Mudzikhala ndi mapemphero othokoza za cipulumutso, ndi kuwalimbikitsa kuti adzipemphera.
- (6) Muwafunse kuti adzipereka umboni wa kulapa kwao monga mungathere kuti adzinena kwa abwenzi ndi okonde-dwa ao (Mateyu 10:32-33).
- (7) Langizani mbusa wanu (kapena ndi kudera kwina, mbusa wina wadela limenelo) za amene amabwerapo, kumapatsa iye nkhani kuti akhoze kulondola anthu ndikuti akhoza kukonzekera za nchito ya mtsogolo.

(1) Muthandizeni kuti atsimikize kusankha Kristu, ndikuthokoza zomwe Kristu anamucitira (1 Yohane 5:13). Iwo akhoza kudziwa kuti Iye anawapulumutsa iwo. John 20:31: "Koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirira kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace."

(2) Aonetseni bwino kupyolera m'mau a Mulungu kuti iwo asanduka zolengedwa zatsopano (2 Akorinto 5:17). Ndikuti ngakhale tipyole m'mayesero omwe angatipange kukhala okaika kapena kuwapanga kuti apatuke pa coonadi, iwo ali ndi mphamvu kugonjetsera zonsezi kupyolera mwa Kristu (1 Akorinto 10:13; 1 Yohane 5:4-5).

(3) Mlimbikitseni ndi kumutsimikizira kuti tsopano tiri m'cisamaliro ca Mulungu atisunga monga nkhoa zace. Ndi Iye mwini amene amatigwira ndi kutisunga ife. Yohane 10:27-29: "Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine. Ndipo Ine ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzaononge ku nthawi yonse, ndipo palibe munthu adzazikwatula m'dzanja langa. Atate wanga, amene anandipatsa izo, ali wamkuru ndi onse; ndipo palibe wina angathe kuzikwatula m'dzanja la Atate."

njano ciyenera kupangidwanso. Kodi inu mwacita zimenezi? Njira yabwino koposa ndiyopanga "m'ndanda-nda wa macimo." Lembani papepala cimo liri lonse lomwe liri lonse lomwe mukuliganizira. Pemphani Ambuye kuti akukumbutseni macimo amene mwawaiwala kapena amene mwawasiya dala. Ndipo gwadani ndikupemphera pemphero liri lonse kufikira onse atakhululukidwa. Imeneyi ndi njira ya kadongosolo ka mtseri ka pakati pa inu ndi Ambuye, kungopatulako ngati munthu wina wakhudzidwa kuti munamucimwira.

2. Kudzikana kotheratu, ndi kufa mwa wekha (Mateyu 16:24-45). Ndikofunika kuti mudziwerengere nokha kuti munafa pamodzi ndi Kristu pa mtanda, ndikuti tsopano ndinu wa moyo kwa Mulungu (Aroma 6:6, 8,11). Tsiku ndi tsiku ziwerengereni kuti mwakhala monga akufa mwa inu nokha, thupi, ndi cimo (Akorinto 15:31).

3. Kudzipereka kwanthunthu kwa Yesu Kristu pomupatsa Iye cifuniro canu. "Cifukwa cace ndikupe-mphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu kuti mupereke matupi anu ansembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa koyenera. Ndipo musafanizire ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikira zimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro" (Aroma 12:1-2). Cimeneci cikutanthauza kuti mumalandira mphamvuyi mwacikhulupiriro mosongozedwa kwanthunthu ndi Mzimu Woyera. Mumadzipereka kwa utsogoleri wace. Pomwe mutacita zinthu zomwe zanenedwazi mudzakhoza kudzazidwa modabwitsa ndi Mzimu Woyera wocitira umboni. Mukhoza kucita za comwe munabadwiranso ngati mutafika pa nsonga imeneyi, ndipo mukhoza kukhala mboni ya Ambuye koposa wotsutsana naye.

**FUNSO LOYENERA KUYANKHANSO NDI NDIME
YOPHUNZIRA**

Mutu Woyamba

1. Kodi ndi makwerero atatu otani odzazidwa nawo ndi Mzimu Woyera? Kodi inuyo makwerero amenewa munacita? Ngati simunatero - citani tsopano musanapitirize.
2. Kodi ndi ndani amene ali citsanzo cathu pocitira umboni? M'njira yotani?
3. Chulani zinthu zikuru-zikuru zomwe ziri m'moyo wanu zomwe zimakulepheretsani kukhala monga momwe Mulungu amafuna kuti muzikhalira. Pitirizani kupanga m'ndandanda wa macimo ndipo gonjetsani cimo liri lonse.

Ndime zophunzira (Poyamba lembani m'nzere pansi pa ndime za m'Buku Lopatulika lanu.),

Macitidwe 1:8: "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: Ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko."

Yesaya 59:1-2: "Taonani, mkono wa Yehova sufupika, kuti sungathe kupulumutsa; khutu lace siliri logontha, kuti silingamve; koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo macimo anu abisa nkhope yace kwa inu, kuti Iye sakumva."

Aroma 6:6: "Podziwa ici, kuti umunthu wathu wakale unapacikidwa pamodzi ndi Iye, kuti thupilo la ucimo likaonongedwe, kuti ife tisakhalenso akapolo a ucimo."

Aroma 6:11: "Cotero inunso mudziwerengere inu nekha ofafa ku ucimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Kristu Yesu."

Mateyu 16:24-25: "Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. Pakuti iye amene afuna kupulumutsa moyo wace adzautaya; koma iye amene ataya moyo wace cifukwa ca Ine, adzaupeza."

5. Timayenera kukumbukira kuti Mzimu Woyera amayenera kupatsa mphamvu uthenga ndi kuti apereke cigonjetso ndi citsimikizo kucoonadi cace. "Uthenga Wabwino wathu sunadza kwa inu m'mau mokha komatunso mu mphamvu, ndi mwa Mzimu Woyera, ndi m'kucuruka kwakukuru; monga mudziwa tinakhala onga otani mwa inu cifukwa ca inu" (1 Atesalonika 1:5).

6. Ife timayenera kukhala ndi makhalidwe monga a Kristu ndi moyo wakuti anthu adzakhala akuona Kristu kupyolera mu utumiki wathu. Ndipo munayamba kukhala akutsanza athu, ndi a Ambuye, m'mene mudalandira mauwo m'citsautso cambiri, ndi cimwemwe ca Mzimu Woyera, kotero kuti munayamba kukhala inu citsanzo kwa onse akukhulupira..." (1 Atesalonika 1: 6-7).

7. Ngati tiri kufuna kupambana, kumafunika kudzipereka m'mapemphero, kuphunzira Buku Lopatulika, kusala kudya ndi kukhala ndi ciyanjano mwa Kristu. "Ndipo anali cikhalire m'ciphunzitso ca atumwi ndi m'ciyanjano, m'kunyema mkate ndi mapemphero" (Macitidwe 2:42).

8. Zinthu zina zofunika kwambiri potsata anthu.

(1) Kucezera mobwereza-bwereza "... Tibwererenso, tizonde abale m'midzi yonse m'mene tinalalikiramo mau a Ambuye tione makhalidwe ao" (Macitidwe 15:36).

(2) Kumakhala nawo pafupi ndi kumawalimbikitsa. "Lalikira mau; cita nawo pa nthawi yace, popanda nthawi yace, tsutsa, dzudzula, cenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi ciphunzitso" (2 Timoteo 4:2; 1 Atesalonika 3:1-2).

(3) Kupemphera kosalekeza kwa tsiku ndi tsiku. "Tiyamika Mulungu nthawi zonse cifukwa ca inu nonse, ndi kukumbukira inu m'mapemphero athu" (1 Atesalonika 1:2).

MAU ENA OTHANDIZAPO POTSATIRA ANTHU

1. PA NTHAWI YOLAPA

MBARI YA CISANU NDI CIMODZI

NCHITO YA MUNTHU WOKOKA MIYOYO KWA MUNTHU WOTEMBENUKA
WATSOPANO

MUTU WA KHUMI NDI CIMODZI

UDINDO WACE KWA MUNTHU WATSOPANO

NDIME ZOYENERA KUGWIRITSA NCHITO POTSATIRA MUNTHU WOLA-
PA TSOPANO

1. Ifetu tiri ndi udindo wothandiza ndi kulangiza aliyense m'njira za Mulungu, kuti tonse tikule. Akolose 1:28: "Amene timlalikira ife, ndi kucenjeza munthu ali yense ndi kuphunzitsa munthu ali yense mu nzeru zonse, kuti tionetsere munthu ali yense wamphumphu mwa Kristu."
2. Ngati cimeneci ciyenera kucitika, tiyenera kukhala ndi makhalidwe abwino pamaso pao (1 Atesalonika 2:11-12) ndikuwauza za Kristu kwa iwo. Agalatiya 4:19: "... Ndirikumvanso zowawa za kubala inu, kufikira Kristu aumbika mwa inu."
3. Tiyenera kukhala ndi makhalidwe a mai amene amadera nkhawa mwana wace kuti akule, kukhala wofera moyo ndi wacikondi ndipo ndi wodzipereka. 1 Atesalonika 2:7-8: "Komatu timakhala ofatsa pakati pa inu, monga m'mene mlezi afukata ana ace a iye yekha; kotero ife poliralira inu, tinabvomera mokondwera kupereka kwa inu si Uthenga Wabwino wa Mulungu wokha, komanso moyo wathu, popeza mudakhala okondedwa kwa ife."
4. Ife timaitanidwa kuti ticitire umboni kupyolera m'moyo wa ciyero, kudzipereka kwa Kristu mwa thunthu. 1 Atesalonika 2:10: "Inu ndinu mboni, Mulungunso, kuti timakhala oyera mtima ndi olungama ndi osalakwa kwa inu akukhulupirira." Kukola miyoyo ndi kuuza ena zomwe Kristu anacita mwa inu ndi zomwe wacita m'moyo wanu.

(Dziwani kuti ngati maphunziro awa aphunzitsidwa mofulumira ndikuti nthawi ndi yocepa ndiponso mwaona kuti simunaphunzire ndime zonsezi pa nthawi ya maphunziro, zisungeni ndimezo ndipo ziphunzireni monga momwe mungathere.)

MUTU WACIWIRI
MAKONZEKELO AKUKOKA MIYOYO

Nchito yaikuru ndi mwai woposa ndi wakuti Mkristu atsogolere M'mzimu wotaika kwa Kristu. Nthawi zina mlaliki wamphamvu ananena za nchito imeneyi kuti, "Mulungu anacita zazikuru ndipo munthu ayenera kucita zambiri koposa nchito iri yonse." Ndi zoonadi kuti ifunikira kukonzekera kwanu kwakukuru. M'madela ofunikira kukonzekera ndi awa:

1. - Cibale Canu ndi Kristu

Cibale canu ndi Kristu ndico cinthu cofunika coyamba kwa wokoka miyoyo. Muyenere kudziwa ndi citsimikizo kuti mukumudziwa Yesu monga Mpulumutsi wanu, nanga mungadziwitse ena za Iye motani? Monga Ambuye Yesu adanena mu Yohane 3:11, "Tilankhula cimene tucidziwa, ndipo ticita umboni za cimene taciona." Iye ayenera kudziwa njira imene akufuna kuti atsogolere ena. Ngati muli ndi cikaiko pa za cipulumutso canu eni ndiye kuti simunakonzekere kukhala ocitira umboni. Cikhulupiriro cacikuru ca pa Ambuye ndi citsimikizo ca zoonadi za Buku Lopatulika cikhoza kulimbikitsa umboni wa okoka moyo ngati utati ukhale wogwira mtima. Munthu wa khungu ndi munthu wokaika sangatsogolere wosapulumutsidwa kucidziwitso ca coonadi ca moyo.

Kodi inu mungadziwe motani kuti munapulumutsidwa-di kapena kuti munabadwanso kwatsopano?

1. Mumadziwa cifukwa Mau a Mulungu anatero:

- (1) Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace" (Yohane 1:12)
- (2) "Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilungamo; ndi m'kamwa abvomereza kutengapo cipulumutso" (Aroma 10:9-10).
- (3) "Izi ndakulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu" (1 Yohane 5:13).

2. Mudziwa cifukwa munapangidwa kukhala watsopano kapena kusinthika:

"Cifukwa cace ngati munthu ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano" (2 Akorinto 5:17).

3. Mumadziwa cifukwa mumakonda abale:

"Ife tidziwa kuti tacokera kuturuka muimfa kulowa m'moyo cifukwa tikondana ndi abale" (1 Yohane 3:14).

4. Mumadziwa cifukwa ca umboni wa Mzimba :

"Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu... Mzimu yekha acita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu" (Aroma 8:14,16).

Ngati inu mutanena monga ananenera Paulo kuti, "Pakuti ndidziwa amene ndimkhulupirira..." mwangocita cofunika coyamba pakucitira umboni.

Potseka gawo iri loyenera kwambiri pezani Macitidwe 22:14,15 kuti muone cifukwa cimene Mulungu anasankhira Paulo kukhala womucitira umboni: "Ndipo anati, Mulungu wa Makolo athu...

2. Fotokozani momwe mungayankhire cifukwa cakuti "mu mpingo muli anthu onyenga ambiri."
3. Fotokozani momwe mungayankhire cifukwa cakuti, "Ine sindingathe."
4. Fotokozani momwe mungayankhire cifukwa cakuti, "Ine ndidzabwera bwino."
5. Fotokozani momwe mungayankhire cifukwa cakuti, "Ine ndine munthu wa mpingo."

Ndime zophunzira (Poyamba lembani nzere pansi pa ndimezi mu Buku Lopatulika lanu,)

Aroma 3:10,12: "Monga kwalembedwa palibe mmodzi wolungama, inde palibe mmodzi... Onsewa apatuka, pamodzi akhala opanda pace; Palibe mmodzi wakucita zabwino, inde, palibe mmodzi ndithu."

Aroma 2:1: "Cifukwa cace uli wopanda mau owiringula, munthu iwe, amene uli yense wakuweruza; pakuti m'mene uweruza wina, momwemo udzitsutsa iwe wekha, pakuti iwe wakuweruza, umacita zomwezo."

Agalatiya 6:7-8: "Musanyengedwe; Mulungu sanyoze-ka; pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzaciduta. Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha."

1 Yohane 5:4: "Pakuti ciri conse cabadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi, ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi;ndico cikhulupiriro cathu."

1 Akorinto 15:57: "Koma ayamikike Mulungu, amene atipatsa ife cigonjetso mwa Ambuye wathu Yesu Kristu."

Yakobo 4:14: "Inu amene simudziwa cimene cidzagwa mawa. Moyo wanu uli wotani? Pakuti muli utsi, wakuonekera kanthawi ndi pamenepo ukanganuka."

wa Mulungu (amene ali Mzimu wa ciuniko) anafuna kukhala mu miyoyo yathu, koma mzimu wa mdima uyenera kucotsedwa. Ndipo ndi Mzimu yekha amene amatsimikiza Yesu kuti ndi Ambuye wocokera kwa Mulungu. "M'menemo muzindikira Mzimu wa Mulungu; mzimu uli wonse umene ubvomereza kuti Yesu Kristu anadza m'thupi, ucokera mwa Mulungu" (1 Yohane 4:2). Buku Lopatulika limanena kuti pali Mpulumutsi mmodzi, Macitidwe 4:12: "... Palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo." Mizimu ya makolo siingathe kupulumutsa moyo wanu, Kodi mizimu ya makolo ikhoza kukuthandizani pa ciweruzo ca Mulungu? Ai! Kodi mizimu ikhoza kulemba dzina lanu mu Buku la Mulungu la moyo? Ai! "Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo, anaponyedwa m'nyanja ya moto" (Cibvumbulutso 20:15).

16. INE NDINE WOKALAMBA KWAMBIRI... LANKHULANI KWA ANA MBALA. Pa mtanda inapulumutsidwa (Luka 23:43), ndipo Mulungu safuna kuti wina aliyense ataike. "(Ambuye) sazengereza nalo lonjezano, monga ena ociyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse, afike kukulapa" (2 Petro 3:9). Yesu sanabwere kudzaweruzo dziko, koma kuti dziko kupyolera mwa Iye likhale nao moyo (Yohane 3:17). Inu tsiku ndi tsiku mumayang'ana nana ndi imfa - ndiponso osati imfa yokha; ciweruzo-nso. "Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa ciweruziro" (Ahebri 9:27). Anthu amitundu yonse, kuli konse, adzaimirira pamaso pa Mulungu. Kodi inu mudzaima motani? (Werengani Cibvumbulutso 20:11-15).

MAFUNSO OBWEREZA NDI NDIME ZOPHUNZIRA

Mutu Khumi

1. Chulani cifukwa zitatu zina zomwe sizinalembedwe, ndipo muikepo mayankho a ndime za m'Buku Lopatulika.

- (1) "Anakusankhiratu udziwe cifuniro cace...
- (2) "Nuone Wolungamayo...
- (3) "Numve mau oturuka mkamwa mwace...
- (4) "Ndipo udzankhalira Iye mboni kwa anthu onse, za izo udazona ndi kuzimva."

Umboni wa mtundu wa gawo lotsirizira umacitika monga zotsatira za magawo atatu ena oyambawo. Cimene-ci ciyenera kukhala moterenso kwa inu. Mukangomudziwa Iye ndi kumva mau ace, umakhala mdalitso ndi mwai wanu wouzako ena za zomwe mwaona ndi kuzimva. Ngati "titamudziwadi Iye" mooni, zotsatira zidzakhala kuti ife tidzafuna kuti tiuze ena za Iye."

2. - Ciyanjano canu ndi Kristu.

Mukakhala ndi ciyanjano ndi Yesu pokhala ndi citsimikizo, mumayenera kukhala m'moyo wa Cikristu

poyanjana ndi Kristu. Ndinu opulumutsidwa ndi Mulungu woyera ndipo mumatumikira Iye. Popeza Mulungu wanu ndi oyera, wacilungamo ndi wowala, Iye sangayanjane ndi cosa-yera, cimo ndi mdima. Cifukwa ca cimeneci yankho ndilo ciyero. "Cifukwa cace, Turukani pakati pao, ndipo patukani, ati Ambuye, ndipo musankhudze kanthu kosakonzeka; Ndipo Ine ndidzalandira inu,

ndipo ndidzakhala kwa inu Atate, ndi inu mudzakhala kwa Ine ana amuna ndi akazi anena Ambuye Wamphamvu yonse" (2 Akorinto 6:17-18).

Kusiyanitsidwa ndi cimo kuli kofunikira cifukwa Mkristu ndi "... kacisi wa Mulungu wamoyo; monga



Mulungu anati; Ndidzakhallitsa mwa iwo..." (2 Akorinto 6:16). Mzimu Woyera sangakhale mu kacisi wosayera.

Umboni woona uli mwa Yesu Kristu, kupyolera mwa Mzimu wace, amene akhala mwa inu. Inu mukhoza kukhala ocitira umboni abwino mumakhala ndi makhalidwe abwino ndi kukhala ndi ciyanjano ndi Yesu. Ciyanjano cimeneci cimatheka bwino mwa kuyeretsewa kwa tsiku ndi tsiku, ndipo cimacitika mwakuphunzira mau ndi mwamapemphero.

Kukhala ndi ciyanjano ndi Ambuye Yesu kudzakupangani kukhala olimba mtima, ndi kucitira umboni mopanda mantha. Citsanzo cakucitira umboni colimba mtima cabwino cili kufotokozedwa mu Macitidwe 4:13. "Koma pakuona kulimbika mtima kwa Petro ndi Yohane, ndipo pozindikira kuti ndiwo anthu osaphunzira ndi opulumukira, anazizwa ndipo anawazindikira, kuti adakhala pamodzi ndi Yesu." Anthu onse amene anasonkhana pamaso pa atsogoleri anazizwa poona kulimbika mtima kwa ophunzira a Yesu. Kulimbika mtima siukali. Kumangonetsa kuti muli ndi ufulu wogawira ena za cikondi ca Kristu (Aroma 1:16). Iwo anali olimbika mtima cifukwa cakuti anakhala ndi Yesu. Inu mukakhala ndi ciyanjano ndi Iye simudzacita manyazi. Mudzakhala ndi kanthu kena katsopano kogawira ena - Ambuye wamoyo. Kumbukirani kuti kucitira umboni sikanthu kena komwe mumacita, koma ndi kanthu kena komwe inu muli - Yesu ali kukhala mwa inu.

3. - Cikondi canu ca kwa anthu.

Ngati inu mulibe cikondi ca pa mizimu kuyesa kwa kucitira umboni kwanu kudzakhala kosabala zipatso ndi kopanda mphamvu. Ndikutheka kuti mudziwa m'mene mungakafikire munthu wina ndi zomwe munganene, koma zonsezi sizingapindule kanthu ngati mulibe cikondi cona ca kwa anthu. Cikondi, kapena kupanda cikondi ndizo zingathandize utumiki wathu. Ngati ife tiri ndi cikondi pa mizimu ya anthu, munthu aliyense amene tingakumane naye akhoza kukhala yemwe tingamuuze za Ambuye Yesu. Wopanda cikondi, zimakhosha kucotsa cinthu ciri conse comwe mungacite. (Tsopano yambani

cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansa pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo." Pali njira imodzi yokha yopulumutsa anthu. Macitidwe 16:31: "Ndipo iwo anati, ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako." Inu muyenera kubadwanso kaciwiri pomulandira Iye, Yohane 1:12-13: "koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupira dzina lace, amene sanabadwa ndi mwazi, kapena ndi cifuniro ca thupi, kapena ndi cifuniro ca munthu koma ca Mulungu."

14. INE NDILIBE NTHAWI KAPENA KUTSUTSIKA. Ngati muli kufuna kusutsika m'thupi mwanu muli kufuna funa cinthu colakwa m'malo oyamba. Buku Lopatulika limaonetsa kuti zofuna za thupi zimatsatilidwa ndi cikhulupiriro (Marko 5:29). Ife timapulumsidwa mwa cikhulupiriro osati zimene akumva! Mzimu Woyera adzatipatsa ife citsimikizo cacikhulupiriro ca cipulumutso. 1 Yohane 5:10: "Iye amene amkhulupirira Mwana wa Mulungu ali nao umboni wa mwa iye." Cimene mungacite ndico kuganizira tsopano m'moyo uno. Popeza ndinu oweruzidwa kale cifukwa cosakhulupirira. "Wosakhulupira waweruzidwa ngakhale dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu" (Yohane 3:18).

15. NDIRI NDI MZIMU UME NE UMANDISUNGA (mizimu ya makolo). M'dziko lino muli mphamvu zambiri, koma Buku Lopatulika limanena kuti iri yoipa ndipo idzati-ononga ife. 1 Yohane 4:1-2: "okondedwa, musankhulupirire mzimu uli wonse, koma yesani mizimu ngati ico-kera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri aturuka kulowa m'dziko lapansi." 1 Timoteo 4:1 "... m'masiku otsiriza ena adzatanga cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda." Aefeso 6:12: "Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimba-na nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a oipa m'zakumwamba. Mzimu

mu Ufumu wa kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa kumwamba." Inu muyenera kumacita cifuniro ca Mulungu ndi kuyanjanitsidwa mwa cikhulu-piriro ca mwa Yesu Kristu. Aroma 5:1: "Popeza tsono tayedwa olungama ndi cikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Kristu."

11. MULUNGU ADANDIPANGA KUTI NDIKHALE MONGA MOMWE NDILILI MU ... KODI NDINGASINTHE CIFUKWA CIANI? Mulungu amene adatilenga ife amanena kuti tiyenera kusankha amene tidzamutumikira ife, "Ndipo ngati kutumikira Yehova kukuipirani mudzisankhire lero amene mudzamtumikira, kapena milungu imene anaitumiki-ra makolo anu okhala tsidya lija la mtsinje ... koma ine, ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikira Yehova" (Yoswa 24:15). Ife sitingatumikire ambuye awiri" (Mateyu 6:24). Ife timakhala kapolo kwa amene tadzipereka tokha (Aroma 6:16). Ife timayenera kusiya ndi kupha zinthu za zilako lako za thupi (Akolose 3:5) ndipo tikhale olengedwa atsopano mwa Kristu. 2 Akorinto 5:17: "Cifukwa cace ngati munthu aliyense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano."

12. INE SINDINAPHUNZIRE KAPENA SINDIMVETSETSA. Mukakhala kuti simunapite kusukulu sindiko kuti simungamvetsetse zoonadi za uzimu. Pokha pokha inu mumvetsetse zinthu za Mulungu. Inu muli ndi khungu ndipo mufunika kuwala. 1 Akorinto 2:14: "Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu; pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwa uzimu." Poyamba ikani cikhulupiriro canu mwa Kristu (2 Timoteo 3:15). Muyenera kumayenda m'kuunika momwe mwayamba-mu.

13. KULI MIPINGO YAMBIRI. Sizimakhala ku mpingo umene inu mumapitako kuti kukukonzere malo amene mudzakhala, koma maganizo anu ndi cikhulupiriro canu mwa Kristu ndico cimabweretsa kubadwa kwatsopano. Pali Mpulumutsi mmodzi yekha. Macitidwe 4:12: "Palibe

mwawerenga 1 Akorinto 13 musanapitirize ndi bukuli.)

Kodi munthu wina akhoza kupeza motani cikondi ca pa mizimuci? Ndi nchito ndi cipatso ca Mzimu Woyera kupatsa cikondi mwa cisomo kwa moyo wa Mkristu. Ndiye kuti ndi Kristu amene akhala mwa inu ndipo iye amakonda kupyolera mwa inu. Ngati inu mulibe cikondi coonadi cofuna kuona ena ali kupulumutsidwa, bvomere-zani cimo limeneli ndikupempha Ambuye kuti akupatseni. "Ndipo uku ndi kulimbika mtima kumene tiri nako mwa Iye, kuti ngati tipampha kanthu monga mwa cifuniro cace, atimvera ciri conse ticipempha, tidziwa kuti tiri nazo izi tazipempha kwa iye" (1 Yohane 5:14-15). Onani kuti zopempha ndizofuna zanu zidziwike kwa iye mu ciyanjano ca tsiku ndi tsiku ndipo cikondi comwe Iye anali naco cidzaonetsedwa kwa inu.

4. - Kumvera kwanu kwa Kristu.

Yeso la pafupi la cikondi canu ndi ciyanjano ca-nu ndi Ambuye Yesu ndi kumvera kwanu. "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga" (Yohane 14:15). Muli kulamulidwa kuti "... mukani kudziko lonse..." (Mateyu 28:19); muli kulamulidwa kutsata Ambuye "... mudzale naye Mzimu" (Aefeso 5:18); mulamulidwa "kuyenda ndi Mzimu..." (Agalatiya 5:25); ndipo lamulo lokhazikika ndilo lakuti "Khalani mwa Ine... wakukha-la mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala cipatso cambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kucita kanthu" (Yohane 15:4-5). Ambuye ayembekeza kuti mumvere zimenezi ndi malamulo ena ambiri kuti akupangani wocitira umboni wobala zipatso, ndipo cipatso ca moyo wa Mkristu ndi Mkristu mnzace. Kufunika kwace kwa kumvera kumaonekera mulonjezano iri: "Ndipo ife ndife mboni za zinthu izi; Mzimu Woyeranso, amene Mulungu anapatsa kwa iwo akumvera Iye" (Macitidwe 5:32).

MAYESO OBWEREZA NDI NDIME
ZOPHUNZIRANSO

Mutu Waciwiri

1. Kodi ndingadziwe bwanji kuti ndidapulumsidwa kapena ai?
2. Nenani zinthu zinayi zomwe Paulo anasankhulidwira kukhala mboni ya Mulungu.
3. Kodi coyenera pa ku "Kuyanjana" ndi Kristu pocitira umboni kuli kotani?
4. Kodi 1 Akorinto 13 amanena kuti cofunika koposa ndi ciani tisanakhale mboni zabwino?

Ndime zophunzira zophunzira (Coyamba lembani mnzere panso pa ndime zimenezi mu Buku Lopatulika lanu.)

Yohane 1:12: "Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace."

Aroma 10:9-10: "Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mu mtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilungamo; ndi m'kamwa abvomereza kutengapo cipulumu-tso."

1 Yohane 5:13: "Izi ndakulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu."

2 Akorinto 5:17: "Cifukwa cace ngati munthu aliyense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano."

Aroma 8:14,16: "Pakuti onse amene atsogozedwa ndi mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu... Mzimu yekha acita umboni pamodzi ndi mzimu wathu kuti tiri ana a Mulungu."

Mbali Yaciwiri
ZIDA ZA OKOKA MOYO

zimakhulupirira. Yakobo 2:19: "Ukhulupirira iwe kuti Mulungu ali mmodzi; ucita bwino, ziwanda zikhulupirira-nso, ndipo zinthunthumira." Koma cikhulupiriro cimeneci ciposa kungoganizira ndi malingaliro a m'mutu mwanu. Sindiko kukhulupirira kanthu kena ka mu mtima mwanu. Timayenera kukhulupirira mu njira yakuti tiyenera kudzipereka tokha kwa Kristu. Luka 14:33: "Cifukwa cace tsono, yense wa inu amene sakaniza zonse ali nazo, sakhoza kukhala wophunzira wanga." Timayenera kumukhulupirira kokwanira kuti tikhoza kusiya macimo athu. Luka 13:3: "Ndinena kwa inu, Iaitu, koma ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonengeka nonse momwemo." Anthu onse ndi ocimwa. Palibe ali yense wa ife ali bwino kuti apulumutsidwe. Aroma 3:12: "Palibe mmodzi wakucita zabwino, inde, palibe mmodzi ndithu." Ife timayenera kukhulupirira mwa Mwana wa Mulungu ndi kuti tipulumutsidwe kucokera ku macimo athu kuti tikhale ndi moyo. Yohane 3:16: "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha kuti yense wakukhulupirira mwa Iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha."

10. INE NDINE CIWALO CA MPINGO KAPENA NDINAPHUNZIRA SUKULU YA MISHONI. (Mwina ena akhoza kunena kuti; "Ine ndidabatizidwa.") Koma funso ndi lakuti, "Kodi inu munabadwanso?" Kukhala ciwalo ca mpingo kapena kubatizidwa sikungakhoze kukupulumutsani. Kungobvomereza ndi mkamwa osati kubvomereza Kristu ndi mtima sikungakwane. Tito 1:16: "Abvomereza kuti adziwa Mulungu, koma ndi nchito zao amkana Iye, popeza ali onyansitsa, ndi osamvera, ndi pa nchito zonse zabwino osatsimikizidwa." Muyenera kucitadi koposa kungokhala ndi dzina. Cibvumbulutso 3:1: "Uli nalo dzina lakuti uli ndi moyo, ndipo uli wakufa." Muyenera kukhala ndi maonekedwe a umulungu, kapena kukhala ciwalo ca mpingo. 2 Timoteo 3:5 "Akukhala nao maonekedwe a cipembedzo, koma mphamvu yace adaikana." Muyenera kucita koposa kungonena mau. Mateyu 7:21: "Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa

8. CIKRISTU NDI BUKU LOPATULIKA ZIRI ZA AZUNGU,
 Buku Lopatulika silinabwere ndi munthu; linauziridwa
 ndi Mulungu. 2 Petro 1:21: "Pakuti kale lonse
 cinenero sicinadza ndi cifuniro ca munthu; koma anthu
 a Mulungu ogwidwa ndi Mzimu Woyera analankhula."
 Lidapatsidwa kuti lipange munthu aliyense mtundu uli
 wonse, kuli konse, "anzeru kufikira cipulumutso"
 (2 Timoteo 3:15). Malembowa ndi mau a Mulungu
 othandiza anthu onse. "Lemba liri lonse adaliuzira
 Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitsa, citsutsa-
 no cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo" (2 Timoteo
 3:16). Buku Lopatulika limatsutsa za cimo (Ahebrei
 4:12) ndikutitsogolera ife kwa Mulungu (Masalmo
 119:105).

Mulungu adalenga anthu onse monga Mlengi;
 cifukwa ca ici anthu onse ali ndi Mulungu mmodzi.
 1 Akorinto 8:5-6 "Koma kwa ife kuli Mulungu mmodzi,
 Atate amene zinthu zonse zicokera kwa Iye, ndi ife
 kufikira kwa Iye; ndi Ambuye m'modzi Yesu Kristu,
 amene zinthu zonse ziri mwa Iye, ndi ife mwa Iye."
 Mulungu saganizira kuti munthu wina ndi wabwino
 kuposa mnzace koma Iye amakonda onse mofanana. Anthu
 onse amayenera kubvomereza cikondi cimeneci ndi
 kumukhulupirira Iye kuti apulumutsidwe. Macitidwe
 10:34-35: "Zoonza ndizindikira kuti Mulungu alibe
 tsankhu; koma m'mitundu yonse, wakucita cilungamo
 alandiridwa naye." Pokhala naye Mulungu mmodzi,
 anthu onse ayenera kumacita mwacikondi ndi mtendere
 kwa wina ndi mnzace. Malaki 2:10: "Kodi sitiri naye
 Atate mmodzi ife tonse? Sanatilenga kodi Mulungu
 mmodzi? Ticita monyangazana yense ndi mnzace cifukwa
 ninji, ndi kuipsa cipangano ca makolo athu?"

9. INE NDI MAKHULUPIRIRA MWA MULUNGU SINDINE WOIPA
 KWENI KWENI. Kawiri-kawiri anthu amafunsa kuti,
 "Kodi pali wina amene angakane Mulungu?" Iwo amati
 "Anthu onse amakhulupirira." Buku Lopatulika limati
 "khulupirira" mwa Mulungu, ngakhale ziwanda

MUTU WACITATU KUFUNIKA KWACE KWA MAU NDI MOYO WODZIPEREKA

Zinthu zofunikira za okoka moyo ziwiri sizikhoza
 kupatukana. Ndikosatheka kugwiritsa nchito cimodzi
 ndi kusiya cina. Kapena kuti cimodzi pa cokha cikhoza
 kukhala ca mphamvu ngati cina citasidwa.

I. - Mphamvu ya Mau.

Mtengo wa Mau a Ambuye pokoka miyoyo siungatheke
 kuyesedwa. Mu Yesaya 55:11 timawerenga otsatirawa
 omwe Ambuye amapanga ponena za Mau ace: "MOMWEMO
 ADZAKHALA MAU ANGA amene aturuka m'kamwa mwanga,
 sadzabwerera kwa Ine cabe KOMA ADZACITA CIMENE
 NDIFUNA, ndipo adzakula m'mene ndinawatumizira."
 Buku Lopatulika ndi mau amene amatumizidwa kudzacita
 cifuniro cake pakati pa anthu. Kupyolera mwa mauwa
 amadzibvumbulutsa yekha kwa munthu ndiponso amabvumbu-
 lutsa makhalidwe a ucimo a munthu. Ndiye kuti Buku
 Lopatulika ndiyo njira imene munthu amapezeramo zosowa
 za cipulumutso ndipo Mulungu adakonza dongosolo lokwa-
 niritsa cosowekaci. Zifukwa zina zomwe Buku Lopatuli-
 ka liri lofunika ndi izi:

1. Buku Lopatulika ndi mbeu.
 Pocitira umboni kwa ena za Kristu, Mau a Mulungu
 ndi mbeu



imeneyi tiyenera kuifesa. Mu Luka mutu wacisanu ndi citatu, Yesu ananena nthano ya ofesa. Yesu potanthauzira nthano ya anati, mitundu yosiyana ya nthaka ifanana ndi mitundu ya anthu omvera ndipo mbeu ndiyo Mau a Mulungu. Cimeneci cinabwelesedwanso mu 1 Petro 1:23, "Inu amene mudabadwanso osati ndi mbeu yofeka, komatu yosaola, mwa mau a Mulungu amoyo ndi okhalitsa." Ndi comveka bwino kuti Mzimu wa Mulungu umagwiritsa nchito mbeu yosaola yomwe iri Mau a Mulungu mu nthaka yaconde ya mu mtima wa munthu kuti ibale cipatso catsopano, palibe ndi mmodzi yemwe angapulumsidwe opanda Mau amenewa. Iye amapereka cionjezero ca cidziwitso, koma wokoka miyoyo okhulupirika ayenera kufesa mbeuzo.

2. Mau ndi mkate kapena mkaka.

Mu Yesaya 55:10 Mau a Mulungu amanenedwa kuti ndi "Mkate kwa owadya." Imeneyi ndi imodzi ya nchito ya Mau a Mulungu pamene munthu afika pacizindikiritso cakudziwa Kristu monga Mpulumutsi. Umenewu ndi mkate weni weni wa Moyo. Yesu anati, "Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha (wathupi), koma ndi mau onse akuturuka m'kamwa mwa Mulungu (mkate wa uzimu)" (Mateyu 4:4). Palibe cina cira conse comwe mwana wobadwa mwa Kristu amacifuna koposa monga cakudya Mkate wa Moyo ndi "Mkaka woyenera wopanda cinyengo, kuti mukakule nao" (1 Petro 2:2). Inu muyenera kudziwa malembo ngati muyenera kukhala okoka miyoyo okonzekera.

3. Mau ndi Lupanga.

Ndi cida codzicinjiriza naco copatsidwa asilikali a Cikristu. "Mutengenso cisoti ca cipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu" (Aefeso 6:17). Palibenso cida cina comwe cingalankhule mozama ndi kuswa mtima kwa munthu, komwe cigonjetso ciyenera kuyamba, koposa mau amenewa, omwe amafotokozedwa kukhala monga "akuthwa koposa Lupanga lakuthwa konse konse" (Ahebri 4:12). Wokoka miyoyo akhoza kupita okonzekera pamene iye atenga Lupanga la Mzimu. Nchito

(Deuteronomo 30:19; Mateyu 6:24). "Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi cuma." Ali yense amapanga lingo lace ndipo adzadziwerengera mlandu yekha. Aroma 14:12: "Cotero munthu ali yense wa ife adzadziwerengera mlandu wace kwa Mulungu." Ciri conse comwe cikukulepheretsani kuti musalandire Yesu monga Mpulumutsi cimasanduka mtengo wa moyo. Mukhoza kukhala ndi cigonjetso pa macimo anu kupyolera m'cikhulupiriro. 1 Yohane 5:4: "Pakuti ciri conse cobadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi, ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi, ndico cikhulupiriro cathu." Posacedwa zinthu za dziko lino zidzacoka. "Ndipo dziko lapansi lipita, ndi cilakolako cace; koma iye amene acita cifuniro ca Mulungu akhala ku nthawi yonse" (1 Yohane 2:17).

6. SINDINGATHE. (Ndidayesa ndidalephera.) Inu mukunena zooni! Inu simungathedi kapena kufuna kopambana poyesa kucita ubwino wanu. Zimatheka kugonjetsedwa ndi mphamvu ya ciyero. 1 Akorinto 15:57: "Ayamikike Mulungu, amene atipatsa ife cigonjetso mwa Ambuye wathu Yesu Kristu." Ndipo "Iye amene anayamba mwa inu nchito yabwino, adzaitziriza kufikirira tsiku la Yesu Kristu" (Afilipi 1:6). Mulungu akhoza kukusungani kuti musalephere (Yuda 24). Moyo wa uzimu umafika pamene Mzimu Woyera akhala mwa inu. Yesu adalonjeza kuti sipadzakhala yeso la mtundu uli wonse lomwe sitingaligonjetse (1 Akorinto 10:13).

7. NDIDZAFIKA KU CHALICHI KAPENA NDIDZAGANIZIRA BWINO. Inu simunalonjezedwe kuti mufika mawa. Yakobo 4:14: "Inu amene simudziwa cimene cidzagwa mawa. Moyo wanu uli wotani? Pakuti muli utsi, wakuonekera kanthawi ndi pamenepo ukanganuka." Tsopano ndi nthawi yokhala opulumutsidwa. 2 Akorinto 6:2: "Tsopano ndilo tsiku la cipulumutso." Inu mukhoza kupulumutsidwa pokha pokha ngati Mzimu wa Mulungu akukukokani. Yohane 6:44: "Kulibe mmodzi akhoza kudza kwa Ine koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye."

Mudzakhala opanda cifukwa copereka. Aroma 2:1; "Cifu-kwa cace uli wopanda mau owiringula, munthu iwe, amene uli yense wakuweruza." Inu mudzakaweruzidwa nokha maso ndi maso. Aroma 14:12: "Cotero munthu ali yense wa ife adzadziwerengera mlandu wace kwa Mulungu." Inu simuyenera kuweruza ena.

Aroma 14:4: "Ndani iwe wakuweruza mnyamata wa mwini wace?" (Agalatiya 6:7: "Musanyengedwe; Mulungu sanyozeka; pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzacituta." 1 Akorinto 3:13: "Nchito ya yense idzaisonyeza, "Kristu ndiye citsanzo cakhalidwe lanu, osati membala wa mpingo. Aroma 2:16: "Tsiku limene Mulungu adzaweruza ndi Yesu Kristu zinsinsi za anthu. "Onse anacimwa, naperewera pa ulemmerero wa Mulungu" (Aroma 3:23).

3. NDIRI KUSANGALALA NDI MACIMO ANGA. Mukhoza kukonda makhalidwe a ucimo, koma dziwani kuti Mulungu adzacita nanu mulandu. Mlaliki 11:9: "Kondwera ndi unyamata wako, mnyamata iwe; mtima wako nusangalale masiku a unyamata wako, ndi monga maso ako aona, KOMA DZIWITSA KUTI Mulungu adzanena nawe mlandu wa zonsezi." Agalatiya 6:8: "Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha."

4. MOYO WACIKRISTU NDIWOBVUTA KWAMBIRI. Ai! Inu ndinu wolakwa. Buku Lopatulika limanena kuti, "Njira ya aciwembu iri makolokoto" (Miyambo 13:15). Yesu anati gori lace ndi lofewa ndi lopepuka. Mateyu 11:28-29: "Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine: cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima; ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu." Yesu amakupatsani mphamvu ndikukuthandizani kuti mukhale ndi moyo wa Cikristu.

5. PALI ZINTHU ZINA ZOMWE SINDINGAZISIYE. Cimeneci ndi cisankho canu pakati pa moyo ndi imfa

yanu ndi yotembenuza otayika kuti acoke mu mdima ndikulowa mukuunika, "ndi kucokera mu ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu" (Macitidwe 26:18). Cinthu cimodzi modzi comweci cinalembedwanso mu 2 Akorinto 4:3-4, pamene Ambuye ananena kuti Uthenga wabwino ubisika kwa otaika cifukwa "... Mulungu wa nthawi yino pa pansu pano unacititsa khungu maganizo a osakhulupirira..." Inu simungathe nkhondo ndi satana mphamvu yanu nokha ndi mphamvu yace; muyenera kukhala ndi lupanga la mphamvu la Ambuye.

4. Mau amenewa ndi kuunika.

Uthenga wabwino ndi kuunika kwa Ambuye komwe amafuna kuunikira m'mitima ya anthu otaika (2 Akorinto 4:4). Buku Lopatulika linenanso kuti "Potsegulira mau anu paunikira..." (Masalmo 119:30). Ndiponso m'ndime ya 105 linena kuti, "Mau anu ndiwo nyale ya ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga." Muzonsezi tiri kuona ulamuliro wa Mau a Ambuye. Cimeneci ndi ciyambi ca Moyo, cakudya cauzimu, mphamvu yogonjetsa Satana m'malo mofuna kuti tibweretse ciwalitsilo ca cipulumu-tso kwa mizimu ya mu mdima. Perekani Mau kwa ena kuti, ngakhale kumwamba ndi dziko zicoka, Mau a Mulungu sadzacoka m'mitima ya amene angamulandire Iye (Luka 21:33). Polankhula mwacigonjetso za zinthu zosatha, gwiritsani nchito Mau, amene adzagonjetsa, ndi kutsutsa ndi kubweretsa zotuta zambiri. Sadzabwerera cabe.

2. - Mphamvu ya moyo wodzipereka.

M'au a Mulungu ndi mpemphero. Kukhala ndi nthawi yogwirizana ndi mphamvu ya Mau a Mulungu m'moyo wanu nthawi ya pa inu nokha ndi Mulungu wanu. Nthawi imeneyi ndi imene Mau a Mulungu amagwira nchito mwa inu, musanayambe kufuna kugawira mauwo kwa ena. Pamenepa, mogwirizana ndi Yesu, mtima wanu umatentha kufuna kuthandiza mizimu yocimwa. Ndipo mumadziphatika pocitira umboni, ndi kwa anthu amene afuna kuti muwacitire umboni, wa Ambuye. Zina za zithandizo ndi zi zomwe zingakuthandizeni.

1. Wokoka miyoyo aliyense ayenera kupanga nthawi ya pa yekha kupanga mtseri nthawi yoikidwa padela. Sayenera kulora kanthu kena kuti katenge nthawi imeneyi. Sayenera kucita kanthu kena katenge nthawi imeneyi. Iyenera kukhala monga kakhalidwe kace ndikukhala yofunikira monga cakudya ca munthu. Mosa-kaika cimeneci cinali cinsinsi ca anthu amphamvu a Mulungu monga Danieli unali makhalidwe ace a mapemphero; Buku Lopatulika limanena za Danieli kuti, "Ndipo podziwa Danieli kuti adatsimikiza colembedwaco, ndipo anagwada maondo ace tsiku limodzi katatu, napemphera, nabvomereza pamaso pa Mulungu wace, monga amacitira kale lonse" (Danieli 6:10). Nthawi yapadela yabwino imene mungakhale nayo kuti mulankhule kwa Ambuye Yesu pa inu nokha ndi kwa inu kukonza nthawiyo. Koma nthawi ya m'mawa ndiyo yabwino kwambiri, pamene muli kungoyamba kukonzekera nchito ya tsiku lace mkhoza kupempha citso gozo ca nzeru ya wam'mwamba. Ciri conse mungacite ndi nthawi yomwe mungacite, fufuzani kuti cikhale cokhazikika m'mapemphero.

2. Wokoka miyoyo aliyense ayenera kudzisankhira malo amapemphero abwino ndi okhazikika. Malowo ayenera kukhala amene mungakhale nokha. Timaona kuti Yesu anali kucita zimenezi pa Mateyu 14:23 "Ndipo pamene Iye anawauza makamuwo, anakwera m'phiri pa yekha kukapemphera: Ndipo pamene panali madzulo, Iye anakhala kumeneko yekha."

3. Wokoka moyo aliyense ayenera kukhazikitsa zinthu m'moyo wace zomwe zingalimbikitse ndikudzizo-weletsa moyo wa mapemphero. Gwiritsani nchito Buku lanu Lopatulika, popeza ndilo cakudya ca mizimu yanu. Liphunzireni mokhazikira. Muzigwiritsa kabuku kapadera komalembamo zinthu zina zomwe Ambuye aliku-lankhula ku mtima kwanu kucokera m'mau ace. Funani funani ndi kudzipereka ku malonjezo odabwitsa a ndime zapamtima. Mudziwerenga mabuku a Cikristu ndi kumaphunzira miyoyo ya Akristu amphamvu omwe anali

lembo litani? Ndipo Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo cinawerengedwa kwa iye cilungamo."

Mutu wa Khumi

MACITIDWE A PA ZA KUPEREKA ZIFUKWA

Malembo Oyera akhoza kupanga wocimwa kukhala wanzeru kufikira pa cipulumutso cace ndi kupanga munthu wokoka miyoyo kukhala wanzeru kuti apindulire miyoyo kwa Kristu (2 Timoteo 3:15). "Ndikuti kuyambira ukhanda wako wadziwa malembo opatulika, okhoza kukupatsa nzeru kufikira cipulumutso, mwa cikhulupiriro ca mwa Kristu Yesu" (Miyambo 11:30). "Ndipo wokola mtima ali wa nzeru." Pa cifukwa ciri conse ciri ndi yankho mu Buku Lopatulika. Cifukwa ca cimeneci tingoyesa kupereka zifukwa zocepa ndi mayankho ace ocokera mu Buku Lopatulika kuyankha zifukwazo. Phunzirani kugwiritsa nchito Buku Lopatulika lanu.

1. INE NDINE WOCIMWA KWAMBIRI. Inde mulidi wocimwa. "Palibe mmodzi wolungama, inde palibe mmodzi... onsewa apatuka, pamodzi akhala opanda pace; palibe mmodzi wakucita zabwino, inde, palibe mmodzi ndithu" (Aroma 3:10, 12). Ciri cinthu cabwino kuti mwazindikira zimenezi, cifukwa anthu ocimwa ndi okhawa amene Mulungu amawapulumutsa, Mateyu 9:12: "Olimba safuna sing'anga ai, koma odwala. "Palibe wocimwa aliyense ali woipitsitsa kuti Ambuye sangapulumutse. "... Kristu Yesu anadza ku dziko lapansi kupulumutsa ocimwa; wa iwowa ine ndine woposa" (1 Timoteo 1:15). Cimeneci ndico comwe Paulo adanena, ndipo ngati iye anali wocimwa wankuru, Kristu akhoza kupulumutsa inunso.

2. MU MPINGO MULI ANTHU AMBIRI ONYENGA. Inu simuyenera kubisala cifukwa ca anthu omwe alephera cipembe-dzo. Inu mudzaweruzidwa nokha pamaso pa Mulungu.

1. Lembani ciphunzitso conyenga cina cili conse comwe mumazidziwa, ndipo perekani yankho ndi ndime.
2. Ngati munthu akhoza kumacita bwino monga angathere, ndi cifukwa ciani sangapulumsidwe?
3. Kodi mamembala onse a mu mpingo ali opulumsidwa? Ngati ndi cifukwa ciani?
4. Werengani Deuteronomo 18:10-12, kodi inu muli okhumudwa ndi cimo lotere? Ngati muli tero likonzeni tsopano.
5. Ndi cifukwa ciani munthu sangapulumsidwe wopanda Kristu?

Ndime zophunzira (Poyamba lembani m'nzere pansi pa ndimezi mu Buku Lopatulika lanu.)

Tito 3:5: "Zosati zocokera m'nchito za m'cilungamo, zimene tidazicita ife, komatu monga mwa cifundo cace anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera."

Agalatiya 2:16: "Koma podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama pa nchito ya lamulo, koma mwa cikhulupiro ca Yesu Kristu, ifedi tinakhulupirira kwa Yesu Kristu, kuti tikayesedwe olungama ndi cikhulupiro ca Kristu, ndipo si ndi nchito za lamulo; pakuti palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi nchito za lamulo."

Ahebri 9:22: "Ndipo monga mwa cilamulo zitsala zinthu pang'ono zosayeretsedwa ndi mwazi, ndipo wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka."

Yohane 14:6: "Yesu ananena naye, ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine."

Aroma 4:23: "Pakuti ngati Abrahamu anayesedwa wolungama cifukwa ca nchito, iye akhala naco codzitamandira; koma kulinga kwa Mulungu ai. Pakuti

okoka miyoyo. Koma tsimikizani kuti pasakhale kanthu komwe kangatenge malo a mapemphero.

4. Wokoka moyo aliyense ayenera kukhala m'guru la mapemphero ndi okhulupirira ena, omwe ali Akristu odzipereka. Mphamvu zazikuru zidalonjezedwa kwa inu ngati mutamvana pa cinthu ciri conse ndi okhulupirira ena motsogozedwa ndi Mzimu Woyera wa Mulungu. Inu mukhoza kulamula kumwamba pamene muli kupemphera m'moyo uno pochula dzina la Yesu Kristu (Mateyu 18:19).

5. Mkristu aliyense ayenera kudziyang'ana kuti asakhale odzinyenga ndi moyo wamapemphero. Dongosolo la la m'ndandanda wanchito ukhoza kukhala monga cimo la

mtseri. Musabise ucimo uli wonse muntima wanu, pakuti ngati mutero Ambuye ananena kuti, "Ambuye sakadamvera" (Masalmo 66:18). Kapenanso kuti mulore zinthu za dziko kuti zisokoneze mapemphero anu potsata zilako-lako zace, kapena pofuna kukhala ngati iwo, kaya zilako-lako za thupi kapena kutsata mzimu wosakhululukira. Pemphe- ro kuti likhale la mphamvu ndi logwira nchito liyenera kucokera



kwa munthu wa cilungamo; ndipo "limacita zamphamvu" (Yakobo 5:16). Mumayenera kukhalanso munthu omvera kwambiri. Kodi mudayamba mwaganizira kuti mukalephera kupereka cakhumi cimakhosha kufoketsa moyo wanu wa mapemphero?

6. Mukamapemphera kweni kweni pa zocitira umboni maganizo awa mwina akhoza kukuthandizani:

- (1) Pemphani Ambuye kuti akutsogolereni kwa munthu kapena anthu ofunikira. Ambuye adzakhoza kuwako-nzeratu mukapemphera ndikufuna utsogoleri wace.
- (2) Pemphani Ambuye kuti akuonetseni malankhulidwe omwe mu ngakalankhule kwa anthu amene ali kukutso-golerani. Muloleni kuti iye alankhule kupyolera mwa inu.
- (3) Pemphani Ambuye kuti akudzazeni mphamvu yomwe akupatsani kuti mulankhule.
- (4) Pemphani Ambuye kuti akhale ali kugwira nchito muntima, pogwiritsa nchito Mau ace pamene inu mwacoka.

Umboni wamphamvu ndi wokhazikika umacitidwa kwa njira ya mapemphero koposa njira ina. Ndizoonadi kuti simungakhale woposa m'mene muliri kopanda moyo wanu wa mapemphero.

MAFUNSO OBWEREZANSO MAU A MULUNGU OPHUNZIRA

Mutu Wacitatu

1. Chulani zinthu zinai zomwe Buku Lopatulika limanena pa za Mau a Mulungu pocitira umboni.
2. Nenani zinthu zinai zoyenera kuzipempherera pamene muli kukonzekera kukoka miyoyo.
3. Kodi mapemphero ena onyenga ndi otani?
4. Kodi lero mwakhala ndi nthawi yotani m'mapemphero? kapena dzulo? Kaya sabata lapita? Bwanji osangodzipangira nthawi ya tsiku ndi tsiku yakuti mudzipemphera?

Ndime zophunzira (Coyamba lembani mnzere pansi pa malembawa mu Buku Lopatulika lanu.):

Yesaya 55:11: "Momwemo adzakhala mau anga amene

Macitidwe timaphunzira za m mene amatsenga ndi ena amene anali kucita zoipa izi adatenthera zinthu zao zaufiti pamene anafika kwa Yesu (Macitidwe 19:18-20).

7. PAKUSAKHALA NDI CIKHULUPIRIRO MU KUUKA KWA KRISTU. Inu simungapulumsidwe pongoganiza cabe kuti Kristu anali munthu wabwino ndikuti pamene anafa anathera pomwepo. Ai! Komabe ena amanena kuti Yesu sanauke. Iwo amanena kuti Iye sanali Mwana wa Mulungu. Yesu anati, "Pamene mwaona Ine, Mwaona Atate." Paulo anati, "kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndikukhulupirira muntima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa udzapulumsidwa" (Aroma 10:9). Ndiponso pa 1 Korinto anati, "Ndipo ngati Kristu sanaukitsidwe, cikhulupiriro canu ciri copanda pace; muli cikhalire m'macimo anu... koma tsopano Kristu waukitsidwa kwa akufa, cipatso coundukula ca iwo akugona" (1 Akorinto 15:17,20).

8. CIPEMBEDZO CINA KAPENA MPULUMUTSI. Kodi monga bwanji za a zipembezozina? Kodi iwo akhoza kupulumsidwa? Buku Lopatulika limati pali Mulungu mmodzi, mlengi wa anthu onse. Ife timadziwa Yesu Kristu kupyolera mwa Mulungu kuti ndi Mwana wace. "Pakuti ngakhaleenso iriko yoti yonenedwa milungu, kapena m'mwamba kapena pa dziko lapansi (monga iriko milungu yambiri, ndi ambuye ambiri), koma kwa ife kuli Mulungu mmodzi. Atate amene zinthu zonse zicokera kwa Iye, ndi ife kufikira kwa Iye; ndi Ambuye mmodzi Yesu Kristu, amene zinthu zonse ziri mwa Iye, ndi ife mwa Iye" (1 Akorinto 8:5-6; Macitidwe 17:24-30). Anthu onse amadziwa Mulungu kuti ndi Mlengi, koma anthu ena adayesedwa ndipo anadzipangira timilungu tamtundu wina, ndipo iwo anataika m'macimo ao, alibe ciyembekezo cacipulumutso (Aroma 1:20-24).

MAFUNSO OBWEREZA NDI NDIME ZOPHUNZIRA

Mutu Wacisanu ndi Cinai

anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo" (Macitidwe 4:11-12). Pali maonekedwe ngati a umulungu, koma ilibe mphamvu za Mulungu (2 Timoteo 4:1-3). Sikwabwino kubvomereza Mulungu podzigwirizanita kukhala ciwalo ca mpingo ngati mtima usanasinthike (Tito 1:16).

5. ANSEMBE KAPENA MUNTHU. Anthu ambiri amafuna kuti munthu adzikhululukira macimo ao. Nthawi zina munthu ameneyu amachedwa wansembe, nthawi zina akhoza kukhala ng'anga kapena munthu wamatsenga yemwe ali ndi mzimu wa mphamvu, koma Buku Lopatulika limati pali mzimu mmodzi yekha amene angapulumutse mitundu yonse ya anthu. "Pakuti pali Mulungu mmodzi, ndi Mtetezi m'modzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiye munthu, Kristu Yesu" (1 Timoteo 2:5). Buku Lopatulika limaticenjeza ife za amene amaika kanthu kena kapena munthu wina m'malo mwa Yesu (1 Timoteo 4:1-3). Yohane anati, "Ndipo akacimwa wina, Nkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye Kristu wolungama" (1 Yohane 2:1). Ndipo Iye ndiye yekhayo amene angatipulumutse ife kucokera ku ucimo. Yesu anati sitienera kuchula munthu kuti mphunzitsi kapena Atate, koma kupatula Atate wa m'mwamba (Mateyu 23:8-10).

6. ZOKOLOWEKA KAPENA ZITHUMWA. Kodi mumadziwa anthu ena amene anagwirizana ndi mpingo ndipo amanena kuti amakhulupirira mwa Kristu, komabe iwo amabvalika ana ao zithumwa ndiponso iwo amabvala zithumwa? Buku Lopatulika limanena kuti kutereku sikuonetsa kusoweka kwa cikhulupiriro coona kokha, koma ndi cimo. Cimeneci sicingathandize kapena kupulumutsa! "Asapezeke mwa inu munthu wakupitiriza mwana wace wamwamuna kapena mwana wace wamkazi ku moto wa ula, wosamalira, mitambo, kapena wosamalira kulira kwa mbalame, kapena wanyanga, kapena wotairika, kapena wobwebweta, kapena wopenduka kapena wofunsira akufa. Popeza aliyense wakucita izi Yehova anyansidwa naye; ndipo cifukwa ca zonyansa izi Yehova Mulungu wanu awapitikitsa pamaso panu" (Deuteronomo 18:10-12). Mu Buku la

aturuka mkamwa, sadzabwerera kwa Ine cabe, koma adzacita cimene ndifuna, ndipo adzakula m'mene ndinawatumizira."

2 Akorinto 5:21: "Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa Iye."

Yakobo 5:16: "Cifukwa cace mubvomerezane wina ndi mnzace macimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzace kuti muciritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'macitidwe ace."

Mateyu 10:32-33: "Cifukwa cace yense amene adzabvomereza Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzabvomereza iye pamaso pa Atate wanga wakumwamba. Koma yense amene adzandikana Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzankana iye pamaso pa Atate wanga wakumwamba."

Ahebri 2:3: "Tidzapulumuka bwanji ife, tikapanda kusamala cipulumutso cacikuru coterere? Cimene Ambuye adayamba kucilankhula, ndipo iwo adacimwa anatilimbikitsira ife."

MUTU WACINAI

M'MENE MUNGAGWIRITSIRE NCHITO BUKU LANU LOPATULIKA

Mu Macitidwe mutu wacisanu ndi citatu Ambuye anatumiza Filipo kukacitira umboni kwa munthu ocokera ku Afrika. Iye anapeza munthu ali kuwerenga Cipangano Cakale ndipo anasendeza pafupi ndikumufunsa ngati anali kumvetsetsa zomwe anali kuwerengazo. Munthuyo anabvomereza kuti sanali kuzindikira, ndipo anali kufuna kuti wina wace amutsogolere. Monga wocitira umboni wabwino, "Filipo anatsegula pakamwa pace, nayamba pa lembo iri, nalalikira kwa iye Yesu" (Macitidwe 8:35). Ndikofunikadi kwambiri kuti wocitira umboni azidziwa kutsegula malembo acoonadi kwa anthu amene sadziwa za Yesu. Zofunikira zogwiritsira Buku Lopatulika ndi izi:



1. Gwiritsani nchito Buku Lopatulika monga cida ca Mulungu. Limeneli ndilo cida. cacikuru ca Mzimu Woyera. Mzimu amagwiritsa nchito yogonjetsera mitima ya anthu kupanda kutero moyo sunga-pulumutsidwe.

2. Gwiritsani nchito Buku Lopatulika monga Cibvumbulutso ca Mulungu. Kulibenso kwina kuli konse komwe kungapezeke makonzedwe a Mulungu a za cimo. Limeneli ndi cibvumbulutso ca yankho loyenera la kwa mtima wa

munthu wosowa. Khalani ozolowera bwino phunziro lalikuru monga: Kucimwa kwa munthu, ciweruzo, Cipulumutso, kulapa, cikhulupiro, kubvomereza ndi moyo wa ciKristu. Mudziyesetsa kuyankha mafunso pomagwiritsa nchito Buku Lopatulika. Osayamba mikangano! Muziyankha mikangano ndi mau a Mulungu. Kunena zoonadi imakonongwa koposa kukwaniritsa zosoweka. Perekani zoonadi za cibvumbulutso ca Mulungu ndipo khulupirirani kuti Iye agwiritsa nchito. Kumbukirani kuti Ambuye sanalonjeze kudalitsa mikangano yanu, koma mau ace! Citsimikizo ca zimenezi cimapezeka mu Yohane 3:34, yemwe ananena kuti, "Pakuti Iye amene Mulungu anamtuma alankhula mau a Mulungu." Zimenezi zinanenedwa pa za Yesu, Komanso zinena kwa munthu okoka miyoyo. Inu muyenera kudziwa ndi kumagawira ena cibvumbulutso ca Mulungu ca Iye mwini ndico Mau ace.

3. Gwiritsani nchito Buku Lopatulika poloweza ndime. Kodi cifukwa ciani kuli kofunikira kuloweza ndime za m'Buku Lopatulika?

Mulungu, pakuti, wolungama adzakhala ndi moyo ndi cikhulupiro; koma cilamulo sicicokera ku cikhulupiro; koma, wakuzicita izi adzakhala ndi moyo ndi izi. Kristu anatiombola ku temberero la cilamulo, atakhala m'malo mwathu, pakuti kwalembedwa, wotembereredwa ali-yense wopacikidwa pa mtengo" (Agalatiya 3:11-13), (Werenganinso Agalatiya 3:24 ndi Aroma 3:20-24; 1 Timoteo 1:9, Ahebri 7:18-19.)

3. MASAKALAMENTI. Anthu ambiri amaoneka ngati kuti amakhulupirira kuti Mgonero wa Ambuye kapena ubatizo umakhoza kupereka cisomo kapena kuthandiza munthu kuti akhale opulumutsidwa. Buku Lopatulika limanena kuti ai! Mipingo ina ili ndi zinthu zambiri zomwe amazicha kuti masakalamenti. Ndipo akamacita zinthu zimenezi zimathandiza kuti munthu apulumutsidwe. Buku Lopatulika limanena kuti ai! Cipulumutso cimabwera kupyolera mu mwazi wa Kristu. "Amene tiri nao maombedwe mwa Iye, m'kukhululukidwa kwa zocimwa zathu" (Akolose 1:14), ndi Ahebri 9:22 amanena kuti: "Ndipo wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka." Yesu ndiye khomo lolowera kumwamba. Njira ina ili yonse ikhoza kutitsogolera ku imfa. "Ine ndine khomo; ngati wina alowa ndi Ine, adzapulumutsidwa..." (Yohane 10:9). Yesu ananenanso kuti: "Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo, Palibe munthu adza kwa Atate koma mwa Ine" (Yohane 14:6). Onaninso pa Yohane 1:12-13,

4. MPINGO. Kodi kugwirizana ndi mpingo kukhoza kupulumutsa? Buku Lopatulika limati Ai! Ai! Ai! Komabe ena amadalira pakugwirizana kwao ndi mpingo kuti apulumutsidwe. Yesu anati, "Si yense wakunena kwa ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba" (Mateyu 7:21). Pamene anthu ali kukana Yesu monga Mesiya ndi Mpulumutsi, cimakhala monga omanga nyumba ali kutaya maziko ace. Buku Lopatulika limati, "Iye ndiye mwalawo woyesedwa wopanda pane ndi inu omanga nyumba, umene unayesedwa mutu wa pangondya. Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina panso, pa thambo la Kumwamba, lopatsidwa mwa

okonzekera kubvomereza zomwe ziri zabwino mwa iwo koma kukhala okonzekera kulangiza zolakwa zao. Ife monga okoka miyoyo tiyenera kudera nkhwana za zolakwika pa njira ya cipulumutso. Ndipo tiyenera kubvomereza apa kuti tikhoza kuyankha mabvuto a uzimuwo.

Amene amakhulupirira mwa cipulumutso kupyolera mwa:

1. NCHITO. Kodi munthu akhoza kupulumutsidwa pocita "ubwino monga angathere," kapena potsatira malamulo a cipangano? Buku Lopatulika limati ai. Aefeso 2:8-9: "Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera ku nchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense." Kapena ndime ina ndi: Tito 3:5 "Zosati zocokera m'nchito za m'cilungamo, zimene tidazicita ife, komatu monga mwa cifundo cace anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera." Yesaya amanenanso kuti: "Zolungama zathu zonse ziri ngati cobvala codetsedwa" (Yesaya 64:6). Paulo amatikumbutsa kuti ngakhale Abrahamu sanapulumutsidwe ndi nchito, koma ndi cikhulupiriro. "Pakuti ngati Abrahamu anayesedwa wolungama cifukwa ca nchito, iye akhala naco codzitamandira, koma kulinga kwa Mulungu ai. Pakuti lembo litani? Ndipo Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo cinawerengedwa kwa iye cilungamo" (Aroma 4:2-3).

2. LAMULO. Alipo anthu ena amene amayang'ana pa Cipangano Cakale, nanena kuti ndikofunikira kumatsata lamulo kuti ukhale opulumutsidwa. Paulo analankhula kwambiri za cimeneci kweni kweni ku mpingo wa ku Agalatiya "Koma podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama pa nchito ya lamulo, koma mwa cikhulupiriro ca Yesu Kristu... pakuti palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi nchito za lamulo" (Agalatiya 2:16). Iye ananenanso kwa iwo kuti: "Ndipo cidziwikatu kuti palibe munthu ayesedwa wolungama ndi lamulo pamaso pa

- (1) Imeneyi ndi njira imodzi yomwe mungaphunzirire mofulumira nzeru yogwiritsira Buku Lopatulika.
 - (2) Imeneyi ndi njira ya mphamvu kwambiri pocitira umboni. Palibe cinthu cina cimagwira nchito monga Mau. Pomaloweza ndime za m'Buku Lopatulika mudzakhoza kukhala ndi kanthu kena muntima mwanu komwe mudzafuna kugawira wina wace, kukhala, "Okonzeka nthawi zonse kucita codzikanira pa yense wakukufunsani cifukwa ca ciyembekezo ciri mwa inu..." (1 Petro 3:15).
 - (3) Ndilofunikira pakugonjetsa cimo. Buku Lopatulika limati: "Ndinawabisa mau anu muntima mwanga, kuti ndisalakwire Inu" (Masalmo 119:11). Cigonjetso ceni, ceni ca pa cimo sicipezeka kopanda Mau.
 - (4) Ndi ofunika kugonjetsa Satana. Pamene Yesu anayesedwa ndi Satana mu Mateyu 4, timaona kuti iye anayamba yeso liri lonse ndi Malembo. Motero potsata citsanzo ca Yesu tiyenera kuphunzira malembo monga tinagthere kukonzekera kukomana nkondo ya Satana ndi timugonjetse ndi Malembo.
4. Kodi ine ndingaphunzire bwino malembo motani?
- (1) Khalani ndi dongosolo lokhazikika bwino. Phunzirani ndime zambiri zabata liri lonse. Sicitenga nthawi, ndipo cimathandiza kusunga nthawi, Inu mukhoza kumaloweza pamene muli kucita zinthu zina kapena kubwera basi. Ambuye akhoza kukuthandizani m'menemo.
 - (2) Phunzirani mu mgwirisane. Gwiritsani ndime pa mutu waphunziro. Mwina mukhoza kuyamba kuphunzira guru la ndime zomwe ananena za cimo, kapena cipulumutso, kapena ciweluzo ndi zina.
 - (3) Phunzirani ndimezo pomabwereza. Bwerezani ndime kamodzi pa tsiku kufikira itakhazikika mwa inu.

5. Gwiritsani nchito Buku Lopatulika poliika m'manja mwa osakhulupirira. Cimakhala cothandiza kwambiri pomuza munthu kuti adziwerengele yekha. Mau a Mulungu analankhula kwa iye molunjika mwina inu mukhoza kutsogozedwa kuti musiye Cipangano Catsopano ngati iye alibe Buku Lopatulika.

6. Mudzilembemo zizindikiro mu Buku Lopatulika lanu. Muzilemba zizindikilo mu Buku Lopatulika lanu kuti mukhoze kumapeza ndime mwamsanga. Pezani dongosolo la kaikidwe ka zizindikiro komwe kangakhale katanathauzo kwa inu. Ngati mwakonza dongosolo lakuti musiya Cipangano kwa munthuyo, ndime zowerengeka zosankhulidwa bwino zikhoza kulembedwamo ndikugwiritsidwa ndi Ambuye.

7. Gwiritsani nchito Buku Lopatulika pokhulupirira Mzimu Woyera kuti atanthauzire coonadi ca Malembo. Wopanda cimeneci munthu wosapulumsidwa sangamvetsetse zoonadi za uzimu. "Koma munthu wa cibadwire ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira cifukwa ziyesedwa mwauzimu" (1 Akorinto 2:14). Munthu osapulumsidwa sangatha-ndizike wopanda Mzimu. Mzimu umathandiza mtima wa munthu kuutembenuza mkati mwace kuti uone coonadi ndi kumubvumbulutsa Yesu yemwe angamupulumutse iye.

MAFUNSO OBWERESA NDI NDINE ZOPHUNZIRA

Mutu Wacinai

1. Chulani njira zisanu ndi imodzi zomwe mungagwiritsire nchito Buku Lopatulika pokoka miyoyo.
2. Kodi ndi cifukwa ciani muyenera kuloweza ndime?
3. Apa nenani zoonadi! Kodi lero mwatenga nthawi yaitali yotani powerenga ndi kuphunzira Buku Lopatulika lanu? Nanga masabata ena apitawo?

yolandiridwa, taonani, tsopano ndilo tsiku la cipulumutso."

Cibvumbulutso 16:15: "Taonani, ndidza ngati mbala. Wodala iye amene adikira, nasunga zobvala zace, kuti angayende wausiwa, nangapenye anthu usiwa wace."

Mateyu 12:30: "Iye wosakhala pamodzi ndi Ine akana Ine, ndi iye wosasonkhanitsa pamodzi ndi Ine amwazamwaza."

Yohane 5:24: "Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti Iye wakumva mau anga, ndi kukhulupirira Iye amene anandituma Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wacokera ku imfa, nalowa m'moyo."

1 Yohane 1:9: "Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse."

1 Atesalonika 5:2: "Pakuti inu nokha mudziwa bwino kuti tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku"

MBALI YACISANU

ZOSAUTSA WOKOKA MIYOYO

Mutu Wa Cisanu Ndi Cinai

M MENE MUNGACITIRE NDI ZIPHUNZITSO ZONYENGA ZA CIPULUMUTSO

Anthu ambiri amakhala ndi maganizo a cipembedzo koma amakhala asanapulumsidwe. Ena anali ndi makolo a cipembedzo kapena iwo eni anaphunzitsidwa pa sukulu la mishoni. Ena analankhulidwa za Buku Lopatulika, Ndipo mu njira zambiri ali ndi maganizo abwino a za Buku Lopatulika, ndipo ena ali ndi zomwe amaganizira kuti ndizo ziphunzitso zao. Ife timayenera kukhala

10:9-10, 13.) Onetsani kufunika kwace kwa kukhulu-
pirika kwa Mulungu pokhululukira ndi kuiwala macimo
athu (1 Yohane 1:9).

PITIRIZANI KULONGOZA KWA KRISTU

Ngati munthuyo ali kuoneka kuti ali kupitiriza
cikaiko ca cipulumutso cace, musangotsimikiza kuti
nchito yatha. Pitirizani kumuonetsa zoonadi zomwe
Kristu adacita ndi zomwe adalonjeza, Ndime zina
zomwe zingagwiritsidwe nchito ndi izi: Mateyu 10:32,
Luka 12:8; Miyambo 28:13. Mukhoza kumulangiza nthano
ya malo ena m'malembo yomwe anthu amene adacimwa
adapeza cikhululukiyo kupyolera mwa cikhulupiriro
(2 Samuel 12:13; Luka 15:18).

MUKHALE NDI PEMPHERO LOTHOKOZA

Limbikitsani munthuyo kuti apemphere, kuthokoza
Ambuye pa zimene Iye anacita. Muuzeni kuti iye
watsegula mtima wace ndipo akhoza kuthokoza Ambuye
mu njira ili yonse yomwe akufuna. Mau sindiwo
wofunika koposa zomwe ziri mu mtima wace.

MAFUNSO OBWEREZA NDI NDIME ZOPHUNZIRA

Mutu Wa Cisanu Ndi Citatu

1. Kodi cifukwa ciani kuli koposa kucedwetsa?
2. Fotokozani nkhanu m'Buku Lopatulika
yomwe munthu wina wocimwa anacedwa ndipo
"sanapulumsidwenso."
3. Perekani citsanzo m'Buku Lopatulika ca
munthu wocimwa kwambiri amene anakhululukidwa.

Malembo Ophunzira (Poyamba Yambani mwalemba m'nzere
pansi pa ndimezi m'Buku Lopatulika lanu.)

2 Akorinto 6:2: "Pakuti anena, M'nyengo yola-
ndiridwa ndinamva ine, ndipo m'tsiku la cipulumutso
ndinakuthandiza; taonani, tsopano ndiyo nyengo yabwino

Kapena mwezi watha?

4. Fotokozani kufunika kwace kwa moyo "wodzipereka"
pokoka miyoyo.

Ndime zophunzira (Poyamba lembani mnzere pansu pa ndime
mu Buku Lopatulika lanu.):

1 Akorinto 2:14: "Koma munthu wa cibadwidwe ca
umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa
zopusa, ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa
mwauzimu."

1 Yohane 1:8: "Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinye-
nga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi."

Yesaya 64:6: "Pakuti ife tonse yakhala ngati wina
amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri
ngati cobvala codetsedwa; ndipo ife tonse tifota
monga tsamba; ndi zoipa zathu zitiuluzwa monga mphepo."

2 Atesalonika 1:8-9: "M'lawi lamoto, ndi kubwereza
cilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera
Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu; amene adzamva
cilango, ndico cionongeko cosatha cowasiyanitsa ku
nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemmerero wa mphamvu yace..."

MUTU WACISANU

ZOKUTHANDIZANI INU NDI ZITSANZO ZOMWE MUNGACITE

Kalongosoledwe ka nchito yocitira umboni kumakha-
la mu njira zambiri ngati utafunadi kukhala wocitira
umboni wabwino. Pali zinthu za zing'ono zambiri zomwe
zinaphunziridwa ndi omwe akhala ali kucitira umboni
zomwe zingakuthandizeni, ndipo mu mutu uno tiyesa
kusonyezamo zina za izo.

1. - YAMBANI NDI PEMPHERO POFUNA KUKACITIRA UMBONI
Pemphani Ambuye yemwe muli kukamucitira umboni

kuti akutsogolereni ndi Mzimu Woyera. Ngati muli kuganizira wina wace, lembani dzina lace pa m'ndandanda wa maina wowapempherera. Khalani ndi pepala lolembedwa comweci ndipo mudzipempherera anthuwo. Komatu, ayenera kukhala amene Mulungu wamuka m'mtima ndi m'malingaliro anu kuti mungawaike papepala lamapemphero anu akhoza kukhala - abwenzi, anansi, abale okhala nao pafupi ophunzira anzanu kapena abwenzi omwe mumayanjana nawo pa zinchito. Mudzipemphera tsiku ndi tsiku, mosalekeza ndi kumabvutikapo. "... pakuti pamene Zioni anamva zowawa, pomwepo anabala ana ace" (Yesaya 66:8).

Pemphani Ambuye kuti atsegule zipata za mitima yawo kuti umboni wanu uwakwanire. Pemphani Ambuye kuti akonze nthaka ya m'mitima yawo kukonzekera mbeu ya Mau. Pemphererani kusaona kwa kutsekeka maso a anthu osapulumsidwa, kuti kusaona kumeneku kucotse-dwa, ndikuti amasulidwe ku mphamvu ya Satana.

2. - MUDZIZIYESA TSIKU NDI TSIKU MAKHALIDWE A MOYO WANU

Umboni wanu sungakhale ndi tanthauzo koposa makhalidwe a moyo anu wa ciyero. "... mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo MUSAFANIZIDWE ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino ndi cokondweretsa, ndi cangwiro" (Aroma 12:1-2).

3. - KHALANI ODIKIRA MWAI WANU.

Mukapempheretsa munthu modzipereka ndi moona, cotsatira ndi cakuti mudziyang'ana mwai wakuti mulankhula kwa munthuyo. Khalani okonzekera mpata ndi mwai umene mwaupempherera. Nthawi zambiri mwayi wa mpata wodzidzimutsa umakhala wobala zipatso, zabwino, komabe, kumayenera kuti nthawi ya mwayi

pafupi kuti aitane pa Yesu kuti alowe mu mtima mwace ndi kumupulumutsa.

KHALANI NDI NTHAWI YOKHAZIKIKA YAKUPEMPHERA YOMWE MUNGAFUNSE MUNTHUYO KUTI APEMPHERE

Iye akhoza kupemphera kuti alape makhalidwe ace a ucimo, popempha Kristu kuti alowe ndi kuyeretsa mtima

wace. Ngati iye sadziwa njira yace yakapempheredwe, kapena ali kukaika-kaika, inu muyenera kumulimbikitsa kuti adzikutsatani pamene muli kupemphera. Nthawi zonse pamene muli kupemphera mukhoza kupemphera motere: "Ndiri kulapa ... kuti ine ndiri ocimwa. Ine sindinga-the kudzithandiza ndekha, ndiri kupempha Yesu kuti alowe mu mtima mwanga, Ine ndikhulupirira,

Ambuye Yesu, kuti munandifera ine, ndiri kukulandirani inu mu mtima mwanga monga Ambuye ndi Mpulumutsi..."

KUTSEKA GANIZO

Pamene muli kuimilira kucoka pa pemphero lanulo, ndi cinthu ca nzeru kulimbikitsa munthuyo kuti afoto-koze momwe apangira ganizo lace kapena alandira malonjezo a Mulungu omupulumutsa iye. Tsimikizani kuti sibwino kukhulupirira ndi maganizo koma ndi cikhulupiriro ca mtima. Gwiritsani nchito ndime za malonjezo a Mulungu zomwe zalembedwa kale (Aroma



(2 Akorinto 6:2b). Ndi nsonga imeneyi yomwe ambiri amapereka zifukwa kuti sayenera kucita zomwe Mulungu wakhoza kuwaululira kuti acite. Phunzirani mutu wa zifukwa, mutatha kuika zizindikiro m'Buku Lopatulika lanu mwakuti Ambuye akhoza kukuthandizani kugwiritsa nchito Mau Ace mokhulupirika bwino. Ndi cinthu cabwino kumulozera ngozi yakucedwa. Mau a nthano zocokera m'Mau a Mulungu ndi zomwe munaona zinacitika zikhoza kuthandiza. (Ndime zina zomwe mungagwiritse nchito ndi izi: Mateyu 25:1-13; Macitidwe 24:25; Luka 12:40; 1 Atesalonika 5:2; Cibvumbulutso 16:15,)

THANDIZANI MUNTHUYO KUTI APANGE GANIZO LABWINO

Palibe ganizo lina labwino lomwe liyenera kutsutsana ndi Kristu. Palibe lingaliro lina lapakati. "Iye wosakhala pamodzi ndi Ine akana Ine" (Mateyu 12:30.) Ngakhale pamene tiri kulankhula ndi cikakamizo pomuitanira kwa Ambuye, sitienera kumukakamiza koterokuti zipangitse munthuyo asatembenukire ku uthenga. Ngati muli kuona kuti palibe cizindikiro ca kulapa kapena kufunitsitsa kuti akhulupirire Kristu, inu simuyenera kucita zomwe Mzimu Woyera sanacite. Mwina ikhoza kukhala njira yofuna kuti inuyo mucoke. Ndipo pambuyo pace Mzimu Woyera akhoza kubweretsa citsimikizo ndi kutsutsa cimo, sizingatheke ndi mikangano kapena cikakamizo canu. Tsogolerani munthuyo kufikira pomwe angafike. Koma mudzikhala acheru pa "liu locepa" lomwe liri kukutsogolerani.

Ngati inu muli ndi citsimikizo cakuti ayenera kufika pacitsimikizo copanga ganizo, mukhoza kuyesa kuwerenga naye Yohane 1:12. "Onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu." Mufunzeni ngati ali kufuna kulandira Yesu ndikuti ali kufuna kumupempha kuti alowe mumtima mwace. Ndipo mukhoza kupezanso Aroma 10:13: "Pakuti amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka." Mupempheni kuti apemphere pemphero la

wanu iyenera kukonzedwa ndikumphereredwa.

Nthawi za mwaizi zikhoza kupangidwa mwa:

1. Cidwi coonadi mwa anthu. Anthu onse amene anakuzungulirani ndi osakondwa, ndipo cidwi coonadi ca kwa anthu amenewa ndico ciri kufunika kuti mitima yao itsegukire Mpulumutsi.

Ocitira umboni ambiri amakhala ndi zinthu zina zomwe zimakondweretsa maganizo ao ndi zofuna za munthu amene akufuna kuti amufikireyo. Pafupi-fupi aliyense amene mungakomane naye ali ndi zomwe zimamupatsa cidwi comwe cingakhale njira zomufikira. Inu muyenera kufuna kuona zokondweretsa zimenezi. Munthu wina anati ngakhale umakonda buledi oika nyama mkati, ngati utafuna kugwira nsomba umadziwa kuti nsomba zambiri zimakonda nyongolotsi. Ngati inu mulibe cidwi coonadi muzokonda za anthu ena, pemphani Mulungu kuti akupatseni.

2. Makhaliidwe a ubwenzi kapena kufikidwa kaulemu. Ambuye Yesu anali a ubwenzi kwa anthu onse, ndipo cifukwa ca cimeneci timaona kuti "Amisonkho onse ndi anthu ocimwa anali kumyandikira kudzamva Iye" (Luka 15:1). Inunso muyenera kukhala aubwenzi kwa onse mudziona kuti zimenezi zidzakupatsani mwai wocitira umboni za Kristu.

Makhaliidwe a nchito zabwino kapena kuonetsa cikondi zidzakhoza kutsegula mitima kuti ilandire ali pa mabvuto kapena cisoni umenewu ukhoza kukhala mwayi wanu kuti mucite ubwenzi kwa iye. Mukhoza kwa iye. Mukhoza kupeza njira yakuti muyambe kukhulupirirana. Yesu anapitapita nacita zabwino" (Macitidwe 10:38). Ndipo ici ndi cosakaikitsa kuti ndico cinali cida cace ku



utumiki wace wamphamvu. Moyo wanu WA CIKRISTU, ngati mutamakhala mocititsa cidwi, udzapatsa cidwi anthu otaika. Cikondi ndi maganizo a utumiki okhazi-kika adzacitira umboni.

3. - MUDZIKHALA AUDONGO M'MAONEKEDWE ANU.

Cimeneci sicofunikira nthawi zonse, cimakhala cofunikira kwambiri anthu ena. Popeza inu ndinu oimira Mfumu ya Mafumu, kaonekedwe kanu ndi kofunika pa moyo wanu - ndipo kakhoza kukhala kopereka ulemu kwa IYE. Mudzikhala okondwa pa njira ya moyo wanu. Nkhope zanu ziyenera kuonetsa kuti muli ndi mtima wokhutitsidwa.

4. - KHALANI OLIMBA MTIMA POCITIRA UMBONI.

Onetsetsani kuti musamacita mantha kapena kukaika. Inu simungathe kukhala ocitira umboni wabwino, kufikira mutayamba mwagwira nchitoyi, mumaphunzira kukhala olimba mtima ndikukhala omasuka polankhula. Buku Lopatulika limenana kuti "Pakuti Mulungu sanatipatsa mzimu wa mantha, komatu wa mphamvu ndi cikondi cidziletso. Conco musacite manyazi pa umboni wa Ambuye wathu" (2 Timoteo 1:7-8). Ambiri amacita mantha, cifukwa iwo amaopa kulephera, kapena zomwe ena amaganiza, kapena amaona kuti sangathe kukwanitsa kucitira umboni. Komatu ngati muli kukhulupirira Ambuye kuti mphamvu yakupezeka yace iri ndi inu simungalephere. Kulimba mtima kumabwera pamene uli kudziwa zosowa za anthu ndi kufunikira kwace kwakuti anthu amve za Yesu. Ngati muli ndi citsimikizo cakuti abwenzi anu ndi akufa ndi ucimo ndipo alibe ciyembekezo popeza ndi otaika ndi opanda Yesu, ndi cifukwa ciyani kuopa? Khalani okhulupirika mu njira yacikondi. Pemphani kuti mukhale olimba mtima. Akhuphunzira anati, "Ndipo tsopano Ambuye, penyani..." (Macitidwe 4:29). Iwo anafuna ufulu ndi mphamvu kucitira umboni wa Yesu. Posacedwa timawerenga yankho la mapemphero awo akuti; "Ndipo m'mene adapemphera iwo..." (ndime

Aroma 3:23 - - "Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu."

Aroma 6:23 -- "Pakuti mphototho yace ya ucimo ndi imfa, koma mphototho yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu."

Yohane 16:8 -- "Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za ucimo, ndi za cilungamo, ndi za ciweruzo."

Aroma 10:13 -- "Pakuti amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka."

MUTU WACISANU NDI CITATU
MASAMALIDWE A UDINDO WA KUZIPEREKA

Ciri cinthu cobvuta kutsimikiza za zosowa cathu mozama kwathunthu pa za utsogoleri wa Mzimu Woyera. Munthu wokonzekera amene amapemphera adzacitira umboni malo okonzeka ndi kwa mtima wokonzekera. Mzimu Woyera amayenera kutitsogolera ife ndi kulangiza mbali ya maganizo athu onse, mwina mwace tikhoza kudzafika pozindikira kuti "tagwira nchito usiku onse ndipo palibe phindu." Ngati inu mwacita zinthu zonse zomwe mtima wanu udayenera kucita mukhoza kudalira Mzimu Woyera kuti akupatseni citsimikizo comwe mungafikire kwa anthu ena. Muyenera kuonetsetsa ndi kutsata utsogoleri wace! Nthawi zonse tiyenera kufunsa munthu amene tiri kulankhula naye za Ambuye kuti afike pa lingaliro la kulandira Ambuye, ngati pali mwai ndikuti Ambuye atsegule khomo, cimeneci ndi comwe ciyenera kupemphereredwa ndi cimenenso tinabwerera MUONETSENI KUFUNIKA KWACE KWA KUPANGA GANIZOLO TSOPANO

"Taonani, tsopano ndiyo nyengo yabwino yolandiridwa, taonani tsopano ndilo tsiku la cipulumutso."

(Macitidwe 16:31). Kukhulupirira sikumangotanthauza kuganizira kokha. Kukhulupirira kumatanthauza kulan-ndira, ndipo kulandirako kumadalira pa malonjezano ace, "Pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye, ADZAPULUMUKA" (Aroma 10:13).

Kukhulupirira sindiko kukhulupirira mu cinthu cocita kapena zongolota kapena zopezeka kale zokhazi-kika zabwino. Kukhulupirira ndiko kukhulupirira nchito yomwe Kristu anaitsirira kale, amene amatitsi-mikizira ife kuti, "Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse" (1 Yohane 1:9).

MAFUNSO OBWEREZA NDI NDIME ZOPHUNZIRA Mutu Wacisanu ndi Ciwiri

1. Kodi cimo ndi ciani? Fotokozani mokwanira.
2. Kodi anthu amatsutsidwa za cimo motani?
3. Kodi ndi ndani anacimwa? Nenani ndime yomwe imanena za ici.
4. Kodi ndi ciani comwe ciyenera pa za macimo athu? Kodi inuyo mutsimikiza kuti mwacitadi njira zonsezi? Ngati simunatero. Yambani mwaima tsopano musapitirize ndiphunziroli kufikira mutaona kuti mwacita cimeneci.

Ndime Zophunzira (Poyamba Yambani Mwalembe Mzere Pansi pa Ndimezi m'Buku Lopatulika lanu.)

Agalatiya 5:19-21 -- "Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenje-zani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu."

31). Anapemphera ndipo analandira mphamvu ndipo anapita nacistira umboni molimba mtima.

5. - GWIRITSANI NCHITO TIMABUKU TATING'ONO.

Mbeu imene muli kufesayo ndi mau a Mulungu. Njira ina imodzi yogwira mtima ndi yogawira timabuku tating'ono ngati zingatheke kupereka pamodzi ndi umboni wanu. Kupereka kanthu kena m'manja a munthu osapulumsidwa kuti awerenge ndi cinthu cofunikira kwambiri. Cimeneci ndicofunikira koposa ngati muli malo opoyera



kapena mwina simungatsatire kufikira ataganiza cocita. Ndi cinthu ca nzeru kuti nthawi zonse mudziyenda ndi timabuku tating'ono m'nthumba mwanu. Anthu ambiri anapulumsidwa atapatsidwa timabuku panjira. "Mamawa fesa mbeu zako, madzulonso osapumitsa dzanja lako; pakuti sudziwa ziti zidzalola bwino ngakhale izizi, ngakhale izozo, kaya zonse ziwiri zizakhala bwino" (Mlaliki 11:6). Onani malamulo otsatirawa akagwiritsidwe ka timabuku tating'ono (Malamulo khumi a kwa

agwiritsa nchito timabuku tating'ono - kucokera kwa American Tract Society.)

1. Musamapatsa timabuku kwa ena musanapemphere. Inu simungathe kupindulira moyo Yesu Kristu wa munthu otaika, ngakhale kabuku kali konse sikangathe. Ndi

Mzimu Woyera yekha angacite nchito imeneyi. Motero tsimikizani kuti mudzipemphera pamene muli kugwira nchito. Pemphani Ambuye kuli akutsogolereni kwa munthu amene Iye alikufuna kuti mumupatse kabukuko. Mupempheni Iye kuti akuthandizeni kusankha kabuku koyenera munthuyo. Pemphani kuti Iye adalitse kabuku-ko ndi owerenga.

2. Perəkani timabuku timene tuli toyenera. Kabuku kayenera kukwanira zosowa za munthu amene wapatsidwayo. Mwachitsanzo simuyenera kupereka kabuku ka zaukwati wosaganizana kwa munthu wokalama.

3. Lankhulani ndi munthuyo. Cimeneci cidzakuthandizani kuti mudziwe zosowa zace ndikuti mukhoza kuthandiza cidwi cace. Yesetsani kumalankhula zinthu zambiri zokhuza Ambuye kuti mukhoza kumupatsa kabuku. Zikhoza kukhala bwino kwambiri ngati iye adzapempha yekha kabukuko. Koma kweni kweni muonetsetse kuti abvomera kukawerenga musanamupatse.

4. Nthawi zonse popereka timabuku muyenera kukhala osangalala. Munthu ogulitsa akatundu amakhala ndi nkhope ya makhalidwe aubwenzi; ogawa timabuku ayenera kukhala oteronso. Nkhope yosakondwa kapena kafikidwe ka mikangano kadzapangitsa munthu owerenga kabuku kutaya cidwi. Ndi cinthu codabwitsa ndiponso cokondweretsa poona kuti timabuku tipereka ndi nkhope ya cikondwerero, anthu sakana kulandira.

5. Musakakamize anthu kuti atenge timabuku monga lamulo, pamene timabuku tuli kuperekedwa mowalanditsa kwa aliyense nthawi zambiri amaperekedwa molakwa. Kuyenda ndi kumapereka bwino kumafooketsa kafalitsidwe ndipondo siumboni wabwino kwa Ambuye.



3. MTSIMIKIZIRENI KUTI YESU YEKHA NDIYE ANGAMUPULUMUTSE IYE

Ngati mphotho yace ya ucimo ndi imfa... ngati onse anacimwa... ngati wina sangakhale wabwino kotero kuti adzipulumutse yekha... kodi pali ciyenbekezo cina cotani? "Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m'menemo, KUTI POKHALA IFE CIKHALIRE OCIMWA, Kristu adatifera ife (Aroma 5:8). Yesu adalipira macimo anu pamene adafa m'malo mwanu. "Pakuti munagulidwa ndi mtengo" (1 Akorinto 6:20). Kristu yekha ndiye adatenga malo athu, popeza Kristu yekha anali wopanda cimo monga Mwana wa Mulungu. Pokhala iye anasanduka munthu, "Ameneyo sanadziwe ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu, kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa Iye" (2 Akorinto 5:21). Mulungu adapereka cipulumutso, koma Iye adapereka njira imodzi - njira yace, kupyolera mwa Mwana wace. "Palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa, nalo" (Macitidwe 4:12).

4. MTSIMIKIZIRENI KUTI PALI ZINTHU ZIWIRI ZIMENE AYENERA KUCITA

Apa khalani osamalitsa kuti iye amvetsetse. Musangokhulupirira kuti iye ali kumvetsetsa mau onse onena za cipulumutso.

1. Patazindikira ndi kubvomereza kuti ali ocimwa, ndikuti ali otaika m'njira za ucimo, iye ayenera kulapa macimo ace onse ndi kutembenuka kucokera kunjirayo mwa mphamvu ya Mulungu. "Ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo" (Luka 13:3). Kulapa kumatanthauza kumva cisoni ndi ucimo. "Nsembe za Mulungu ndizo mzimu wosweka, Inu Mulungu simudzapeputsa mtima wosweka ndi wolapa" (Masalmo 51:17).

2. Popeza mwatembenuka kucoka m'njira za ucimo tsopano "KHULUPIRIRANI AMBUYE YESU, ndipo udzapulumuka"

6:23). Cimeneci ndico cifukwa cace Kristu adafa. Iye anatenga malo athu a imfa. Cimo limalekanitsa. "Pacilango Mulungu adzadzibvumbulutsa yekha, milawi la moto, ndi kubwezera cilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu; amene adzamva cilango, ndico cionongeko cosatha cowasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemmerero wa mphamvu yace" (2 Atesalonika 1:8-9). Anthu amafunika kudziwa coonadi ca ciweruzo ca Mungu komanso ayenera kudziwa za cipulumutso ca cikondi cace.

2. - MTSIMIKIZIRENI KUTI SANGATHE KUDZIPULU-MUTSA YEKHA

Cikhoza kukhala bwino kugwiritsa nchito miyambi ya mu Buku Lopatulika kuonetsa kuti ndikosatheka kudzithandiza tokha. Coonadi ndi cakuti, ndi nthawi yokhayo imene tingabvomere kuti tisowa thandizo lomwe tingathandizidwe nalo. Kudziyeretsa tokha sikungathandize (Yesaya 64:6). Nchito zabwino sizingapindule kanthu (Aefeso 2:8-9). Kumvera ndi kusunga malamulo sindiyo njira ya cipulumutso (Aroma 3:20). Pofotokozera nsonga zimenezi mukhoza kugwiritsa nchito nthano ya mnyamata mwini cuma cambiri (Mark 10:17-31). Kapena nthano ya Nikodemo (Yohane 3:1-16).

Kumaganiza kuti tiri abwino kopambana munthu wina, kapena osati oipa ngati anthu ena amene amapita ku chalichi, ciri cisonyezo cakuti tiri kusowa coonadi ndikuti tifunika kudza kwa Kristu Yesu. Yesu anenana kwa Afarisi kuti, "Mukadakhala osaona (kubvomereza kulakwa kwanu) simukadakhala nalo cimo, koma tsopano munena, kuti, tipenya: cimo lanu likhala" (Yohane 9:41). Mukhoza kufotokozera poonjezera kuti munthu otaika ali monga munthu omila pa madzi. Iye akamapitiliza kuyesa-yesa kuturuka m'madzimo mwa iye yekha pomwe anamira patali. Ngakhale "kungokhulupirira" kuti kuli cingwe comwe cingamupulumutse sikungamupulumutse. Iye ayenera kugwira cingwe ndi pamene iye ayenera kulandira cipulumutso comwe cinapatsidwa kwa iye monga mphatso yaulere ya Mulungu.

Nthawi zonse ndi cinthu cabwino kugawa timabuku khumi ndi awiri mosamala bwino, mwamapemphero ndi mwacinwemwe koposa kumapereka Zana kwa anthu mopanda dongosolo.

6. Mudzigwiritsa nchito timabuku topatsa cidwi. Inu - ndi Ambuye wanu - mudzaweruzidwa ndi zida muli kuzigwiritsa. Nthawi ya timabuku tosindikizidwa monga pepala la nkhani ndi kulembedwa motaipidwa ndizopanda nthano idapita. Masiku ano inu mukhoza timabuku kucokera kumipingo yanu kapena kwa anthu ena amene ali ndi makina odindwa. Mudzigwiritsa nchito timabuku tomwe tudalembedwa bwino, wosalakwika, mosalembedwa ziphunzitsa zina ndi zolakwa zina.

7. Sungani timabukuto. Onetsetsani kuti mapepala a timabuku ali osungidwa mwa udongo ndiponso oyera bwino pamene muli kupereka kwa ena. Timabuku tikakhala m'nthumba mwanu masiku awiri kapena atatu tudzapangitsa kuti tusaoneke bwino.

8. Mudzigwiritsa timabuku tabwino tothandiza kumanga nchito ya Ambuye. Pewani tumabuku tomwe tumanena zoipa za mipingo ina kapena guru lina. Nchito yathu yakufuna kudzionetsera, koma kupereka coonadi ca uthenga wabwino.

9. Ganiziranitu njira zatsopano zogwiritsira timabuku. Gwiritsani nchito timabuku pa nthawi ya nchito ku makampani ndiponso pomalemba makalata mukhoza kuikamo kabuku kaya pokapereka ngongole, popereka makadi a mafuno abwino, ndi m'mabuku amene mumabwereka abwenzi. Mukhoza kuwatumiza m'mainivolopi, ngakhale kwa anthu amene simuwadziwa. Mudziika timabuku pomwe anthu angakhaze kuwanyamula ndi kuwawerenga mosabvuta. Khalani okhazikira m'makhalidwe anu ndipo funani funani njira yatsopano zogawirira timabuku kwa ena.

10. Yambani tsopano kugwiritsa kabuku tsiku ndi tsiku. Lekani kuganizira za nthawi imene mungadzaga-

wire timabuku zana pa sabata limodzi mwina sangabwere. Yambani kuwagwiritsa nchito kabuku kamodzi tsiku ndi tsiku, ndipo mudzadabwa ndi madalitso omwe Ambuye adzakudalitsani nao pa nchito yanu ndikukhutitsidwa komwe mudzakhale nako.

6. - Zinthu zofunikira zoyenera kucita ndi zosayenera kucita.

1. Zinthu zina zoyenera kukumbukira pocita nchitoyi:

- (1) Gwiritsani Buku Lopatulika lanu. Ligwiritsemi m'manja mwanu ndipo mudzilongoza ku ndime polankhula.
- (2) Nthawi zonse khalani okhazikika. Dekhetsani liu lanu polankhula. Khalani wacimwemwe. Lolani kuti Mzimu wa Mulungu agwire nchito kupyolera mwa inu. Musamusokoneze pokhala pa njira yacifuniro canu.
- (3) Khalani ndi cidwi ndi anthu amene ali patsogolo panu.
- (4) Ndi kwabino kumagwira nchito ndi guru la msinkhu wanu. Ngati ndinu mtsikana, ndiye muyenera kugwira nchito ndi atsikana. Mnyamata agwire nchito ndi anyamata. Azibambo agwire nchito ndi azibambo. Mzimai agwire nchito ndi azimai. Ngati mukhoza kugwira nchito ndi wina wace wa msinkhu ndi guru la mtundu wina, pemphani Ambuye kuti akupatseni nzeru zapadera, ndipo yesetsani kupita ndi munthu wina. Musamacheza ndi munthu waguru lina nokha (wamwamuna kuceza ndi mkazi wekha.)
- (5) Gwirani nchito ndi munthu mmodzi pa nthawi imodzi. Onani kuti, zacipulumutso liri dongosolo lapadera. Ndi mtima umene umayenera kubadwa.
- (6) Pitilizani kuloza kwa Kristu. Mudzinena

timaona ucimo m'miyoyo yathu ndi m'miyoyo ya ena monga zocita cita za thupi. Ndipo nchito zathupi zionekera: ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kanduka, zopysa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mzeco, ndi zina zotero (Agalatiya 5:20-21). Ngati zimenezi ziri cimo, kodi ndi ndani anacimwa?

2. Inu ndinu ocimwa! "Onse anacimwa, naperewera pa ulemmerero wa Mulungu" (Aroma 3:23). Ndi cinthu cotheka kwa munthu kukhala wa khungu ndikukana kuona cimo lace, koma Buku Lopatulika limanena kuti, "Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi" (1 Yohane 1:8). Munthu amene amadziyeretsa yekha - ngakhale pa nchito zabwino ndi zacilungamo - amapezeka wocimwa ndi Mau a Mulungu, amene amanena kuti, "Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri ngati cobvala codetsedwa" (Yesaya 64:6).

3. Kuopsya kwa cimo. Muyenera kumuonetsa kuti pali ngozi yaikuru popitiliza kukhalabe ndi makhaliidwe wa ucimo wopanda Kristu. Buku Lopatulika silimangone na kokha kuti Mzimu Wace "Udzakhala uli kubvutika pamodzi ndi anthu," koma limalankhulanso za malo athu pamaso pa Mulungu. Yohane amanena kuti, "Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupira WAWERUZIDWA NGAKHALE TSOPANO, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu" (Yohane 3:18). Yohane anapitiliza kunena kuti, "Iye amene akhulupirira Mwanayo ali nao moyo wosatha; koma iye amene sakhulupirira Mwanayo sadzaona moyo, koma mkwiyo wa Mulungu ukhala pa Iye" (Yohane 3:36). Pali ngozi inanso. Kupitiliza kukana kumatanthauza kulimbitsa moyo. Ndipo ukalimbitsa moyo umakhala opanda ciyembekezo. "Yemwe aumitsa khosi atadzudzulidwa kwambiri, adzasweka modzidzimuka, palibe comciritisa" (Miyambo 29:1).

4. Zoturuka M'cimo. Nthawi zonse zimo limabwe-reysa manyazi. "Mphotho ya ucimo ndi imfa" (Aroma

KUPEREKA NJIRA YA CIPULUMUTSO

Kodi inu muli ndi zinthu zakale zomwe mungagawirane ndi anthu ena? Kodi muli ndi cidwi pa zimene Kristu anacita m'moyo wanu pokhululukira macimo anu, kukupulumutsani kucokera kuciweruzo, ndi kukulonjezani moyo wosatha? Pali zinthu zambiri zomwe munazipeza pamene munabwera kwa Kristu. Njira ya cipulumutso sindiyo ya matsenga pofuna kupulumutsa anthu otaika. Ndi njira yogawira ena kupyolera pa zomwe munazona pamene munadza kwa Yesu mutaona mkhalidwe wanu woipa. Munadziona nokha kuti munalibe ciyembekezo monga wocimwa ndipo Mulungu adakonza njira kuti akupangeni kukhala mwana wace. Mzimu Woyera ndiye amene anakufikitsani pamalo amenewa. "Adzatsutsa dziko lapansi za macimo, ndi za cilungamo, ndi za ciweruzo" (Yohane 16:8). Mulungu anatilonjeza ife umboni wa Mzimu Woyera pogawira ena uthengawu pofuna kubweretsa miyoyo kwa Iye yekha, ndi kuwatsutsa pa za njira za ucimo kuti apulumutsidwe.

1. - KUTSUTSA OCIMWA ZA MACIMO

Anthu onse kuli konse amazindikira ndi kudziwa za cimo. Coonadi cakuti tiri ocimwa ciri pamaso pathu. Anthu ena saganizira kweni kweni kuti cimo ndi ciyani ndikuti limacita ciyani.

1. Kodi cimo ndi ciani? Buku Lopatulika limanena kuti, "Yense wakucita cimo acitanso kusayeruzika; ndipo cimo ndilo kusayeruzika" (1 Yohane 3:4). Komanso limanenanso kuti, "Potero kwa iye amene adziwa kucitanso bwino, ndipo sacita, kwa iye kuli cimo" (Yakobo 4:17). Ndiponso limanena kuti, "Cosalungama ciri conse ciri ucimo" (1 Yohane 5:17). Cimo limadzionetsa lokha mu njira zosiyana siyana, koma limafotokozedwa kuti ndi kucita cifuniro codzikonda pocita mosemphana ndi cifuniro ca Mulungu. Yesaya anati cimo ndikuti "Tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha," (Yesaya 53:6). Ife

zacikondi canu ca pa Iye.

- (7) Pemphani mosalekeza, ngakhale panthawi imene muli kulankhula ndi kuwerenga ndime za malamulo, mtima wanu udziitana Mulungu kuti agwire nchito ya cisomo m'moyo mwa munthu ali patsogolo panu.

2. Zinthu zina zosayenera kuzicita:

- (1) Osakangana nao. Imeneyi ndiyo njira imodzi yalepherera. Kapena mwina mukhoza kulephera ndi mkanganowo, kapena kulephera kukhala bwenzi la munthuyo. Inu mukhoza kumapambana mikangano yonse, ndipo mukhoza kumalephera kubweretsa anthu kwa Yesu.
- (2) Musamalankhula monyoza mipingo ina kapena zipembedzo zao. Kumbukirani kuti munthuyo aliku-sowa cipulumutso ndipo ali pangosi yacitaiko asowa Mpulumutsi. Timayenera kulankhula za Yesu, osati kukangana wina ndi mnzace.
- (3) Yesetsani kusunga mkwiyo wanu bwino. Ena akhoza kumanyoza, kukucepetsani ndi kukunyodolani. Akhoza kupeputsa cikhulupiriro canu ndi kuseka Ambuye wanu. Cimeneci cisakudetsani nkawa, ndipo musamayankha mwacisoni.
- (4) Musamafulumira. Imeneyitu ndi nchito yofunika koposa. Khalani ofatsa. Zipatso za moyo wongobadwa m'banja la Ambuye ndiyo phindu lake.
- (5) Usamanena zosiyana ndi kabuku. Padzakhala yeso lofuna kukupatutsani pa coonadi. Khazikikani pa coonadi canu! Onetsetsani m'mene anthu anali kuyesela Yesu ndikuti asiye kuloza za cimo, koma Iye anali kumawatengela pa cimo.
- (6) Musamakakamiza nkhani. Sungani nkhani ya za ubatizo ndi nkhani ya za ubatizo ndi kukhala ciwalo ca mpingo kufikira nthawi ina. Khazikikani pa nkhani yomwe iri yofunika kwambiri -

cipulumutso ca munthuyo.

- (7) Musamaika nchito zabwino zanu kuti zichinjirize njira. Khalani odzicepetsa, samalirani kuti musayese za kukhala oyera koposa makhalidwe anu.
- (8) Musalore kuti luntha lanu licoke mucidziwitso canu. Musamayesa kuyankha mafunso omwe simuli kuwadziwa kayankhidwe kace. Khalani okhulupirika. Tengani nthawi imeneyi kuiyesa ya mwai odziwitsa munthuyo kwa mbusa wanu kapena munthu wina yemwe amadziwa mau kwambiri.
- (9) Musamamva mantha. Kumbukirani kuti mukhoza kukhala olimba mtima ndi kukhala wa cimwemwe.

MAFUNSO OBWEREZA NDI MALEMBO OWERENGA

Mutu Wacisanu

1. Kodi njira yoyamba ndiyotani, kuti ukhale oyenera kukoka miyoyo usanayambe?
2. Kodi ndikhoza kukhala ndi mwai motani pokoka miyoyo?
3. Lembani malamulo asanu onena za kagwiritsidwe ka timabuku.
4. Chulani zinthu zinai zoyenera kucita ndi zinthu zinayi zosayenera kucita pocitira umboni.

Ndime zoyenera kuphunzira (Poyamba lembani m'nzere pansi pa ndimezi m'Buku Lopatulika lanu.):

Aroma 12:1-2 "Cifukwa ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: Koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cambwino ndi cokondweretsa, ndi cangwiwo."

anu. Pemphererani nthawi ya mwayi yakuti mukalankhule nawo.

2. Lembani cinthu ciri conse comwe muli kuganiza kuti cikhoza kukuletsani kuti musalankhule nawo. Pempherani kuti Ambuye akuthandizeni kuti mucigonjetse, ndi kucicotsa kapena kuti atsogolere munthuyo kwa wina yemwe ali wokonzeka.
3. Fotokozani za munthu yemwe munali naye ndi zomwe zinacitika pofuna kupindula moyo wace.

Ndime zophunzira (Poyamba yambani kulemba mnzere pansi pa ndimezi m'Buku Lopatulika.):

Aefeso 2:8-9: "Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro;ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu: cosacokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense."

Yohane 3:16: "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wokukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha."

Yohane 3:18: "Wokhulupirira Iye saweruzidwa. wosakhulupirira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu.

Yohane 3:36: "Iye amene akhulupirira Mwanayo ali nao moyo wosatha; koma iye amene sakhulupirira Mwanayo sadzaona moyo, koma mkwiyo wa Mulungu ukhala pa iye."

Yohane 3:3: "Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu."

MBARI YA IV

WOKOKA MIYOYO NDI MUNTHU WOTAICA
MUTU WA CISANU NDI CIWIRI

zachulidwa kale mu mutu wina. Tsimikizani kuti mau a timabuku ali kunena za mutu wofunikawo.

6. - MUDZIYENDA NDI MTIMA WOTHODWA NDI WOLEMA

Kumapeto kwa mutu uno, kumbukirani kuti munthu wosapulumsidwa adzadziwa ngati inu munakonzekera bwino mau anu. Khalani omasuka. Koposa zonse muzilankhula zomwe mudazona ndi zomwe munamva komatu ndi mkhalidwe womumvera iye cisoni. "Akubzala ndi mizosi adatuta ndi kufuula mokondwera. Iye ayenda yenda nalira, ponyamula mbeu yakufesai adzabweranso ndithu ndikupfuula mokondwera alinyamula mitolo yace" (Masalmo 126:5-6). Ndikoyeneradi kuti pofika kwa munthu mudzifika ndi mtima wothodwa. Mudzisungiratu mau a ndime yace mu malingaliro anu. "Ngati inu mukomoka pa tsiku la mdani, mphamvu yanu imacepa. Ngati inu musamalira kufuna kupulumutsa amene ali pafupi ndi imfa, ndi amene ali pafupi kuphedwa, ngati inu mutanena kuti, Taonani, ife sitinadziwa; kodi iye amalora kuti mtima wace uganizire? Ndipo iye amene amasunga moyo wako, kodi iye sadziziwa izi. Ndipo kodi iye sazabwereza kwa munthu aliyense molingana ndi nchito yace?"

Alipo anthu ambiri amene anagwidwa ndi msampha wa Satana amene ali kusendzedwa ku imfa ya uzimu - abwenzi anu, anthu amene amakhala mu mzinda wanu. Inuyo ndinu amene muli ndi mankhwala a ciombolo: Uthenga wa Ambuye Yesu Kristu. Ife sitinganene kuti, "Taonani ife sitidziwa bwino." Koma ngakhale tikada-khoza kutero: "Kodi amene adakonza mitima yathu sadziwa ici bwino?... ndipo iye sadzabwezera kwa munthu aliyense molingana ndi nchito yace?"

MAFUNSO OBWEZERA NDI ZOPHUNZIRA Mutu Wacisanu ndi Cimodzi

1. Lembani m'ndandanda wa maina khumi wa anthu amene muli kuwadziwa kuti sanalandire Kristu monga Mpulumutsi. Alembeni pa pepala la mapemphero

Macitidwe 16:31: "Ndipo iwo anati, ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako."

Luka 13:3: "Ndinena kwa inu, Iaitu koma inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo."

Aroma 5:8: "Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa, Kristu adatifera ife."

Macitidwe 4:12: "Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansu pa nthambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo."

MUTU WACISANU NDI CIMODZI MAFIKIDWE ANU

Iye monga Mkristu tsopano muyenera kukhala otsimikiza kuti mudzicitira umboni; ndiponso Ambuye wanu adzakudzazani ndi mphamvu yocitira umboni ngati mwakonzekera kudzipereka kwathunthu. Komanso muyenera kuzindikira kuti Ambuye analonjeza kuyenda nanu ndikukhala nanu ndipo zimungalephere. Inu mwaphunzira Mau ndi kupemphera. Pamene muli kuyamba nchito yocitira umboni tsopano, pali malamulo ena amene tiyenera kuwatsata.

1. - PITANI MTSOGOLO

"Ndipo tsopano muka, ndipo Ine ndidzakhala m'kamwa mwako ndi kukuphunzitsa comwe ukalankhule" (Eksodo 4:12). "Ndipo ananena nao, Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse" (Marko 16:15). Inu mulikulamulidwa kupita ca mtsogolo; khalani pa nchito ya Atate wanu. Inu simungapindule moyo wa munthu kufikira mutayamba kucita. Ngati mwaphunzira maphunziro anu mwadziwa



zambiri zoti mukhoza kuyambira nazo. Dzipitani komwe muli anthu. Musamangoyembekezera kuti munthu abwere kwa inu. Mu mutu woyamba wa Yohane timawerenga m'mene (ndime 35 - 40). Mau otsatira ndime zimenezi pa (ndime 41) pali mau akuti, "Anayamba iye kupeza mbale wace yekha Simoni." Iye anamupeza. Cimeneci citanthauza kuti anapita kwina nayamba kukamufuna funa iye, ndikumubweretsa kwa Yesu. Munthu wina amene anafikiridwa anali Filipo." Ndipo Yesu

ananena naye, Tsata Ine. "(ndime 43). Cimeneci cica-dacitika ndi Yesu yekha pomapita kumene anali kupita. Cotsatira apo, "Filipo anapeza Natanayeli," (ndime 45). Iye anamufuna atamupeza anamubweretsa iye kwa Yesu. Amene ali olimba safuna sing'anga; koma akudwala ndiwo (Luka 5:31).

2. - DZIWANI BWINO ANTHU OSOWA CITHANDIZO,

Ngati kungakhale kotheka, mukhale mutadziwa kale mbiri ya munthu amene muli kufuna kukalankhula naye. Dziwiranitu dzina lace, nchito imene amagwira, zomwe zimakondweretsa ndi za cipembedzo cace ngati anali m'cipembedzo kale. Nthawi zambiri mabanja kapena abwenzi akhoza kukupatsani nkhani zambiri ya miyoyo yao. Ngati wocitira umboni ayesa kucitira umboni kwa amene sadziwa bwino za moyo wace yambani mwalankhula naye nkhani zina kufikira mutadziwa zina zace za iye. Mudzimvetsetsa mosamala kwa munthuyo. Mudzimulola kuti alankhule. Ndipo mukhoza kuyamba

nkhani yacipembedzo. Miyoyo ya anthu iri ya mtengo wapatali simuyenera kungofika mopanda dongosolo labwino. Yesetsani njira iri yonse kuti mudziwe bwino mbiri ya munthuyo ndi maziko ace. Mutatero ndiye kuti zidzakuthandizani kuti mucite zolakwa polankhula.

3. - KHOTETSANI NKHANIYO KU NSONGA YOFUNIKIRA

Cimeneci cimayenera kukhala cizolowezi. Ndi cinthu cabwino kumagwiritsa nchito nkhani zozolewerekamonga momwe Yesu analankhulira ndi makazi pa citsime mu Yohane 4. Iye poyamba anamupempha madzi akumwa, ndipo anaikotetsa nkhaniyo ku "madzi a moyo." Samalirani kuti simuyenera kupereka lingaliro lakuti muli kuzemba mutu wa nkhani. Nthawi zambiri mukhoza kufikira pa mutu wa funso lakuti, "Kodi munapempha Yesu kuti alowe muntima mwanu?" Kapena kufunsa kuti "Kodi muli kufuna kudziwa tanthauzo lakukhululukidwa kwa macimo anu?" Nthawi zambiri sibwino kucita ngati muli kubisa mutu wa nkhani, komatu muyenera kukhala omasuka polankhula ndi onena moonadi.

4. - KHALANI OPATSA CIDWI NDI OKHAZIKIKA M'MALANKHULIDWE

Malankhulidwe abwino amatanthauza kuti muzilankhula zinthu zoyenera mu mzimu wofatsa. Mukazolowera nchito bwino poigwira mumafika bwino kwa anthu ndipo magwiritsidwe a nchito ndiye mphunzitsi. Kafikidwe kaufulu kwa munthu kamabweretsa cikhulupiriro kwa wakumvayo. Cidwi ndi cikondi canu apa cikhoza kuonjezera cidwi cakufuna kuti amve mau a Mulungu. Kukhulupirika ndi kunena moonadi kumapangitsa kuti munthu amene muli kulankhula nayeyo akhale ndi cidwi pa zomwe muli kumuuzau mau. Kawiri-kawiri ngati munthu ali kudziwika kuti sakhalira kupysa mtima kapena kuti amakhumudwa mwamsanga, njira yabwino yoyamba naye ndiyo yakumufotokozera kuti kodi Yesu amatanthauza ciani kwa inu.

5. - GWIRITSANI BWINO TIMABUKU

Njira imeneyi kawiri kawiri iri yabwino monga